


KUBZALA MPESA NDI KOMWE MUNGAWUBZALE IWO

 Ife tiri ndi zinthu zambiri, koma Inu mukudziwa mtima wathu ndipo mukudziwa chirichonse chimene ife tikuchisowa. Ndife okondwa kwambiri kuti ife tikhoza kubweretsa izo kwa Inu mu pemphero, podziwa kuti Inu mukumvetsa ndipo mupereka kwa ife za ubwino Wanu; osati kuti ndife oyenera izo, koma chifukwa Inu munalonjeza izo kwa ife. Ndine wotsimikiza kuti pali zopempha zambiri mu mpingo mmawa uno, za matenda ndi osowa. Ndipo ife modzichepetsa tingawabweretse iwo kwa Inu pakali pano, kupempha chifundo Chanu chabwino ndi mphamvu yamachiritso, kwa aliyense wa iwo.

² Ife tikupemphereranso kuchira ndi iwo amene sanathe kufika ku tchalitchi mmawa uno. Komanso, kwa ambiri amene asonkhana pano tsopano. Ambiri akudwala ndi osowa. Ife tikuwawona iwo ali ndi ndodo ndi mmipando, ndi zikuku, ndipo iwo aku—iwo akusowa chifundo Chanu. Ife tikupemphera, Ambuye, kuti Inu mupereke izo kwa iwo, mochuluka. Mulole iwo atuluke muno, akusangalala, ochiritsidwa ndi abwino. Ambiri omwe sakuwonetsa kusautsika kwawo, koma, komabe, mwinamwake vuto la mtima liri pafupi kuti liwatenge iwo, kapena khansa, kapena chiwanda china chowopsya. Ife tikupemphera, Ambuye, kuti iye aponyedwe kutali mmawa uno. Iwo achoke pano, okondwa, ali bwino.

³ Ife tingakumbukire mnyamata wamng'ono ameneyo amene—amene akufa. Zinangowuzidwa kwa ife, ndi wokondedwa, amene ali ndi khansa ndipo amwalira lero, ngati chifundo Chanu sichifalikira kwa mwana ameneyo. O Ambuye Mulungu, muchitireni chifundo mnyamata wamng'ono ameneyo. Mpatseni iye chiwombolo, Ambuye; ngati izo ziri chomwecho mu chifuniro Chanu Chaumulungu. Ndife okondwa kwambiri chifukwa cha umboni wake, kuti iye wavomereza Magazi Anu, mochuluka kuti anawapempha abambo ake kuti amuyike m'manda atavala zofiira, kuti iwo adziwe kuti iye anaphimbidwa ndi Magazi. Ife tikukuthokozani Inu, Ambuye, chifukwa cha chikhulupiriro chochirimika cha ngwazi zazing'onozo, kumagunda chitsogolo kukakumana ndi mathero a moyo, kukumbatira ku mitima yawo mtanda, ndipo pamenepo kuwonetsera chilemba cha Magazi. Ngati zonse zitakhala zotheka, Ambuye, mutetezeni mnyamata wamng'onoyo, muloleni iye akhale moyo. Ife tawapempherapo ena.

⁴ Ndiyenso, Ambuye, ife tikupempherera misonkhano mmawa uno. Pali ena pano, mwinamwake, amene samakudziwani Inu ngati Mpulumutsi wawo. Ngati izo ziri chomwecho, mulole ili likhale tsiku limene iwo akupezeni Inu ofunika ku moyo wawo, monga Mpulumutsi. Iwo amene akusowa machiritso, akupezeni Inu ngati Mchiritsi. Ambuye, Inu mubwere kwa wantchito Wanu, mmawa uno. Ndiroleni ine ndikupezeni Inu ngati Mlaliki. Pakuti, ife tikupereka zonsezi kwa Inu, kupempha kuti Inu muyankhe mu Dzina la Ambuye Yesu. Amen.

⁵ Timakhala okondwa nthawizonse kubwera m'nyumba ya Ambuye, ndi ku Msonkhano wa Woyamba kubadwa. Ndipo ine, monga mwachizolowezi, ndinachedwa. Sindimaganiza kuti ndifika kuno, apo ayi ndikanakwera matola. Iyi ndi nthabwala yabwino kwa mkazanga. Iye wakhala mkati muno, penapake. Iye ananyamuka mmawa uno, ndipo ine ndinali pansu mu chipinda chapansi ndikuwerenga. Ndipo iye anati, "Ine ndatenga makiyi, Billy." Ndipo ndinadzapeza kuti, iye anatenga makiyi aku garaja, aponso. Sindinathe kukalowa. Ndinali ndi nthawi yovuta.

⁶ Ndipo patapita kanthawi, Billy anandisowa ine, ndipo iye anati, "Ndikudabwa chifukwa chimene iye sanabwere." Ndipo iye anandiyimbira ine.

⁷ Ine ndinati, "Iwe ubwere mwamsanga ndithu." Ine ndinati, "Chifukwa ine ndiribe njira yobwerera ku tchalitchi." Chotero ife tiri...Ndine wokondwa kukhala pano. Chotero, ine ndachedwa.

⁸ Koma, inu mukudziwa, pamene ife tidzafika mu gawo linalo, kumene sikudzakhalanso nthawi, ife tidzayamba kuyiwala za nthawi. Izo zonse zidzalowerera mu Muyaya, ndipo sikudzakhalanso nthawi. Sikudzakhalanso malire a nthawi.

⁹ Paulo akuyenera kuti anali ndi chinachake chonga chimenecho m'maganizo mwake, usiku umene iye analalikira usiku wonse. Mnyamata anagwa m'nyumbamo ndipo zinamupha iye. Ndipo Paulo anayika thupi lake pa mnyamatayo, ndipo moyo unabwerneranso kwa mnyamatayo.

¹⁰ Ndikukhulupirira ndawuzidwa, ndi abusa, pompano, kuti ali ndi mwana wamng'ono amene akufuna kuti adalitsidwe mmawa uno. Chotero ngati amayi angamubweretse mwana wamng'onoyo, pompano, ife timupereka iye kwa Ambuye, wamwamunayo kapena wamkazi, chirichonse chimene iye angakhale. Ndipo ine ndimakhala ngati ndimakonda mautumiki a kuwadalitsa. Kodi inu mungabwere patsogolo, M'bale Neville?

¹¹ Mmawa wabwino, mlongo. Dzina la mwanayo ndi ndani? [Mlongo akuti, "Frank Wayne Dabney."—Mkonzi]. Frank Wayne Dabney. Iwe sungakhale pachibale ndi Robert Dabney, sichoncho iwe? Frank Wayne Dabney, ali ndi zaka zingati? ["Masabata eyiti."] Masabata eyiti. Sanakhale m'dziko

lankhazali nthawi yayitali. Chabwino, iye ndi chipatso cha chilumikizano chanu. Ndipo tsopano inu mukufuna kuti mumupereke iye kwa Mulungu, kuti iye akhale wantchito Wake. Nkulondola uko, mlongo? Mulungu akudalitseni inu.

¹² Chabwino, ine ndanyamula chuma chaching'ono apa, wokongola kwenikweni. Tangoyang'anani pa izo, Frank Dabney wamng'ono.

Tiyeni tipemphere.

¹³ Wokonedwa Atate Akumwamba, mmasiku akuyenda Kwanu pano pa dziko lapansi, mmawonekedwe a munthu, wotchedwa Ambuye Yesu, iwo anabweretsa kwa Inu ana aang'ono. Ndipo Inu munayika manja Anu pa iwo ndipo munawadalitsa iwo, ndipo munati, "Lolani ana adze kwa Ine, ndipo musawaletse iwo, pakuti wotere uli Ufumuwo." Mayi yu akumpereka mmikono yanga, mmawa uno, mnyamata wamng'ono uyu, amene ine ndikumpereka kwa Inu. Ndikupemphera, Ambuye, kuti Inu mumudalitse mwana wamng'onoyo. Mudalitse nyumba yake. Mulole iye aleledwe mnyumba ya Chikhristu. Mu kumuwopa Mulungu, mulole iye aleledwe. Ndipo ngati kuli mawa, mulole iye adzalalikire Uthenga ngati iye ali wodzozedwa chotero ndi Inu. Mpatseni iye moyo wautali, wathanzi. Mudalitse makolo ake. Mulole chinthu chabwino chirichonse chimene Inu munalonjeza, chibwere pa mnyamata wamng'ono uyu. Amayi amupereka iye m'manja mwathu, monga akulu a mpingo. Ndipo tsopano ife tikumupereka iye kwa Inu. Mu Dzina la Yesu Khristu, Inu mumudalitse mwana yu. Amen.

Mulungu akudalitse iwe, Frank wamng'ono. Ndikuganiza kuti iwo ndi okoma kwambiri!

¹⁴ Ine ndimayenera kuwapempherera iwo pamene ine ndiri ndi kudzoza...?..Ife tiri ndi mipango yina pano yoti ipemphereredwe, koma ine kulibwino ndichite zimenezo ife tikayamba kupempherera odwala, ndipo kudzoza kwa utumiki kutabwera. Ndiye zingadzakhale bwino ngati titadzawapempherera iwo nthawi imeneyo.

¹⁵ Wokondwa kuwona ambiri a abwenzi anga ali muno. Ine ndikukhulupirira ine ndikumuwona M'bale Charlie Cox kumbuyo uko mu msonkhano. Ndipo ine ndikumuwonanso M'bale John O'Bannon, wochokera ku Louisville. Ndi abwenzi ena ambiri, ozungulira, omwe ine—ine ndikuwazindikira. Ndipo chotero ndife okondwa kukhala nanu inu, kusunkhana nafe mmawa uno, kuti tiwatumikire Ambuye.

¹⁶ Tsopano ife tikuyembekezera, pakapita kanthawi, kuti tiyambe chitsitsimutso kuno kwa masiku angapo. Tikupemphera kuti izi zitheke. Ine ndikumverera kuti ngati Mulungu sangabweretse chitsitsimutso, kapena kuyika icho pa mtima wathu, ndiye chitsitsimutsocho ndi kuyetsesa kwathu kwathu.

Ndiyeno ngati ife titadikirira, ndipo Iye nkumverera kuti ndi nthawi ya chitsitsimutso, ndiye Iye nkuziyika izo pa mtima wathu, ndiye ife tidzamverera kuti tikhale ndi chitsitsimutso.

¹⁷ Mzanga wina amene wakhala pano, abambo ndi amayi a M'bale Wood, ndi mmodzi wa matrastii athu pano pa tchalitchi. Ndife okondwa kukhala nawo iwo mmawa uno.

¹⁸ Ndipo ndikupita kumusi mu msewu, dzulo, mwamuna amene ankakhala kuno mu mzinda, ameneyo anali munthu wamng'ono wovuta kwambiri. Ndipo nthawizonse ndinkamukonda iye, ndipo mnyamata wabwino. Ndipo mkazi wanga ankakhala moyandikana nawo. Ndipo iye anali ngati woyimba, ndi wa zing'wenyeng'wenye. Ndipo iye anakonda kukhala pamene ndi kumamenyetsa phazi lake, atavala chipewa chachikulu cha wolishya ng'ombe, ndi zosewerera. Koma iye ankagwira ntchito ku WPA. Ndipo tsiku lina chinachake chinachitika, chimene nthawizonse chimandikumbutsa ine, kapena ndachisunga mmalingaliro anga, kani, kwa nthawi yaitali. Icho sichinachokebe. Iye anali ndi ana aang'ono angapo; mkazi wokonedwa. Iwo anali osauka monga momwe kusauka kungakhalire, monga ife tonse tiriri.

¹⁹ Ndipo ine ndinawona, nditayima pa sitepe, atafola, akuyembekezera kuti cheke cha WPA chija chibwere. Wodzasiya makalata anabwera mumsewu. Iwo anali osangalala kwambiri. Tsiku lotsatira linali Isitara. Iwo amati akagule maswiti ena a Isitara kapena chinachake, pamene cheke cha adadi chibwera. Ndipo pamene wodzasiya makalata anabwera, iye analibe cheke cha adadi. Inu mukuona maonekedwe okhumudwa amenewo pa nkhope za ana aang'ono amenewo, ndipo izo nthawizonse zinkandikhudza ine, kukhumudwa koteroko.

²⁰ Ine ndinaphonya kumuwona mwamunayo, kwa zaka. Ndipo dzulo, ndikubwera kumusi mu msewu, pamene ine . . . Mkazanga ndi ine timatuluka mu sitolo yayikulu, kapena Quaker Maid kumusi kwa tawoni, ndinakumana ndi ndani, maso ndi maso, koma iyeyo? Ndipo chimodzi mwa zinthu zoyambirira zomwe iwo amafuna kundiuza ine, iye anali atakhala Mkhristu. Iye sanamwe kwa zaka. Ndipo ndine wokondwa kukhala nanu, Bambo Logston, akhala pa mpando wakutsogolo, muno mu tchalitchi, mmawa uno. Iye ndi membala wa mpingo wa M'bale Junior Cash ku Charlestown, Indiana, m'bale wabwino kwambiri. Ndikwabwino kwambiri kukhala Mkhristu kuposa momwe ziliri kunjā uko mdziko. Sichoncho izo? Tsopano, ine ndikuganiza iye amaimba pa maprogramu, ndipo amayimba zing'wenyeng'wenye zake, kwa ulemelero wa Ambuye. Basi chikho china cha chisomo chodabwitsa cha Mulungu.

²¹ Kodi mungafune kuti mungoimirira, Bambo Logston? Ine sindi . . . Mwamuna ameneyu nthawiyina anali chidakhwa. Mmodzi wa ovina mmalo azisangalalo awa, inu mukudziwa,

zoseweretsa ndi zinthu. Tsopano izo zonse zatebenezidwira ku Ufumu wa Mulungu, ndipo iye ali kunjira kuno, akuti, “Zikomo Inu, chifukwa cha izo, Ambuye.” Oh, pamene . . .

²² Ine ndimawauza Bambo Wood, dzulo. Ine ndinati, “Pamene inu ndi amayi, mukadzafika kutsidya lina ndi kudzatenga nyumba yanu yayikulu, ndipo mmawa wina pamene inu mudzakhale wokondwa kwenikweni, ndipo kumusi komwe kutsidya kwa mapiri, ndi kulowa mu dzenje, kwinkwake, kumene kuli kanyumba kakang’ono komangidwa kumeneko. Ndikadzatulukira pakhonde, ndi kudzafika ndi kudzaima pakhonde, ndidzafuula pa mayenje onsewo:

Chisomo chodabwitsa! kumveka kwake
nkokoma bwanji,
Chopulumutsa watsoka ngati ine!
Ndinatayika nthawiyina, ndipo tsopano
ndapezeka,
Ndinali wakhungu, koma tsopano ndikuwona.

²³ Ine ndinawauza Bambo Wood, ine ndinati, “Chabwino, mudzawasisite amayi paphewa, mudzati, ‘Mulungu alemekezeke! M’bale Branham wakale wakwanitsa izo. Ndi uyo apo, kumusi uko mu kanyumba kake kakang’ono.’” Ngati ndidzafike konse Kumeneko, zidzakhala mwa chisomo chodabwitsa cha Ambuye Yesu.

²⁴ Tsopano kodi ife tingaweramtse mitu yathu mphindi yokha tisanatsegule Mawu.

²⁵ Ambuye ndife chinachake ngati gulu la ana. Tiri ndi mawonekedwe athu aumunthu, ndipo, ife, kuseketsa kwathu, chiyanjano chathu pamodzi. Tsopano ife tikubwera ku gawo lopatulika kwambiri limenelo la utumiki uliwonse, kuti tiwerenge Mawu osalephera a Mulungu wamoyo. Ine ndikupempha, Ambuye, kuti Inu muyankhule ndi Mawu aliwonse. Mulole Iwo apite ndi kudzamira mmitima ya anthu, ndi kudzakolola zokolola zomwe zinkalingaliridwa. Mulole Mzimu Woyera wawukulu ubwere pakati pathu tsopano, ndi kudzatenga Mawu awa amene ati awerengedwe, ndipo muwagawe Iwo kwa ife, payekhapayekha, monga ife tikusowera. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu ndi chifukwa Chake. Amen.

²⁶ Mu Masalmo wa 80, ine ndikufuna kuti ndiwerenge kagawo.

Tcherani khutu, O M’busa wa Israeli, inu amene akutsogolera Yosefe ngati nkhusa; inu . . . wokhala pakati pa akerubi, walani.

Pamaso pa Efraimu . . . Benjamini ndi Manase kondowezani mphamvu zanu, ndipo mubwere mudzatipulumutse ife.

Tibwezeninso ife, O Mulungu, . . . muwalitse nkhope yanu; ndipo ife tidzapulumuka.

O AMBUYE Mulungu wa makamu, kodi inu mudzakwiyira mapemphero a anthu anu mpaka liti?

Inu mukuwadyetsa iwo ndi mkate wa misozi; ndipo mukuwamwetsa iwo misozi yambiri mu muyezo wochuluka.

Inu mutipangitsa ife kulimbana ndi mnansi wathu: ndipo adani athu amaseka mwa iwo okha.

Tibwezereninso ife, O Mulungu wa makamu, . . . muwalitse nkhope yanu; ndipo ife tidzapulumutsidwa.

Inu munatanga mpesa kuchokera ku Igupto: inu munathamangitsa wamitundu, ndipo mwabzala iwo.

27 Phunziro langa mmawa uno, ngati Ambuye alola, kwa kanthawi kochepe chabe, likhala pa: *Kubzala Mpesa Ndi Komwe Mungawubzale Iwo.*

28 Ndi zachirendo momwe Mulungu, mmalo ambiri, amawaimirira anthu Ake mwanjira zosiyanasiyana. Osati kale kwambiri ife timayankhula pamene Iye anatiimirira ife ngati mphungu, ndipo Iye pokhala Mphungu Iyemwini, ndipo ife mphungu Yake yaying'ono. Ndipo ndikudalira kuti zonse ziyenda bwino. Nthawi yomaliza yomwe ndinalankhula za zimenezo, ndinalandira kalata. . . Mzinda wawukulu uja, ambiri a inu mukudziwa kumene iwo unali, mu Ohio, kuti bungwe la azitumiki linasonkhana pamodzi ndi kutsutsa mautumiki anga chifukwa ine ndikukhulupirira kuti Mulungu anamuyitanira munthu ku Moyo Wamuyaya maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Ndipo mwa kukhulupirira kwanga, ngati Mulungu ali Mulungu, anakhalapo Mulungu, Iye akadali Mulungu, ndipo nthawizonse anali Mulungu. Ngati Iye sanandidziwe ine dziko lisanakhalepo, ndiye kuti Iye si Mulungu.

29 Ambiri a inu mwakhala mukuwerenga pano pabwalo lachiwonetsero, ndi zina zotero, pa malingaliro apamwamba awa. Ndipo zina za izo, ndithudi, zinabwerera ku utumiki wanga. Koma, ngati munaphunzirapo kapena munali ndi njira iliyonse yophunzirira zanthano, nthano: “chinachake chomwe chimawoneka ngati chiripo, koma palibepo.”

30 Ndipo mu Malemba, ife tikupeza kuti Yambre ndi Yane anamutsutsa Mose pochita chinthu chomwecho chimene iwo ankachita, kuponyera pansu ndodo ndi kuisandutsa kukhala njoka. Mose anaitanitsa miliri. Ndipo iwo ankatha kuyitanitsa miliri, nawonso, koma iwo sankatha kuichotsapo miliriyo. Iwo sakanakhoza kuchiza, chifukwa Mulungu ndi mchiritsi yekhayo. Koma iwo anakwanitsa kuibweretsa miliri, kenako

Mose ankaichotsapo iyo. Kenako chiwonetsero chomaliza chinabwerapo, pamene Mose anachita monga momwe Mulungu anamuuzira iye.

³¹ Ndipo ine ndikudziwa, zonse izi zomwe ziri pafupifupi, mu dziko lero, potsiriza zidzafika ku chiwonetsero chimodzi chachikulu tsiku lina. Chifukwa, Baibulo linati, “Monga Yane ndi Yambre anatsutsana ndi Mose, momwemonso anthu amalingaliro okanika adzatero, zokhudza Chikhulupiriro, adzatsutsa m’masiku otsiriza, koma kupusa kwawo kudzawonekera.” Ndi uneneri womwe ukuyenera kukwaniritsidwa, ndipo inu mukhoza kuwona mbali ziwiri zonse zikuwuka tsopano.

³² Koma Mose anachita ndendende basi chimene Mulungu anamuwuzira iye kuti achite. Iye anaponyera pansi ndodoyo ndipo inasanduka njoka. Ndipo am’bwebwe awa anatulukira ndipo anadzaponyera ndodo zawo pansi ndipo izo zinasanduka njoka. Mose anali kumapeto kwa luntha lake, ndi kumapeto kwa mphamvu zake.

³³ Koma pamene ndi pamene Mulungu amafuna kutitengerapo ife, basi kumapeto kwa ulendo wathu, kenako Iye amabwerapo. Ndizo chimodzimodzi monga Iye. Mwinamwake inu mukudwala kwambiri, mmawa uno, mpaka adokotala akuti inu simungakhale moyo. Munthu yemwe akumira mmadzi amakagwira udzu. Umo ndi momwe zimakhallira pamene tiyesera kupeza...Zonse zomwe tingathe kuzichita, ifeeni, zomwe ziri zaumunthu, izo ife tidzazichita. Koma pamene zifika pamalo pomwe palibe chiyembekezo china, iwo amene samakhulupirira mu machiritso Auzimu amakhulupirira nthawi yomweyo. Chimadzakhala chiyembekezo chawo chokhacho.

³⁴ Ndipo Mose anali kumapeto kwa kufikira kwake, kenako Mulungu anabwerapo ndipo anadzapangitsa njoka yake kudya njoka ya munthu winayo. Kenako njoka yake panalibenso.

³⁵ Tsopano, mu kuzindikira kwapamwamba, ndi mu zanthano, ndi azamizimu onse. Ndiroleni ine, basi ine ndisanayambe pa mutu wanga, ndikuwongoleleni inu ndi ichi, mwa thandizo la Mulungu, ngati ine ndingathe. Mdierekezi akhoza kupangitsa kuti zinthu ziwoneke zolondola, koma nthawizonse zimatsimikizira kuti siziri zolondola. Tsopano, iwo sanakwanitsepoko konse kupeza chithunzi cha iliyonse ya mizimu iyi apa yomwe yawonekerapo, chifukwa iyo kwenikweni palibepo pamene.

³⁶ Koma pamene inafika nthawi yoti Mulungu atsimikizire kwa sayansi, Iye anali Mulungu, Iye analola kuti chithunzi chijambulidwe. Icho nchoti sichingafwifwe. Wofufuza anati, “Kuwala kunagunda magalasi. Kuwalako ndithudi kunali pamene. Izo sizinali kuwerenga maganizo.” Chotero, inu mwaona, chimene Mulungu amachita ndi chokhalitsa.

³⁷ Njoka ya Mose inameza njoka ya enawo. Ndipo iye amakhoza kuinyamula iyo mdzanja lake, ndipo njoka yawo inali mkati mwa ndodo imeneyo. Zomwe mdierekezi amachita ndi nthano. Zimene Mulungu amachita ndi zenizeni. Chotero, ndimakonda izi kuti zimire mozama mmitima. Pamene Mulungu apulumutsa munthu, iye amapulumsidwa. Musadandaule za kubwereranso mmbuyo; inu simungathe. Chimene Mulungu amachita ndi Chamuyaya. Mdierekezi akhoza kugwira ntchito pa inu ndi kukupangitsani inu kukhulupirira kuti ndinu wopulumutsidwa. Koma pamene Mulungu akupulumutsani inu kwenikweni, inu mumakhala nacho icho bola ngati icho chiripo, chifukwa inu muli nawo Moyo Wamuyaya. Yesu ananena chomwecho.

³⁸ “Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine ali nawo Moyo Wamuyaya, ndipo sadzabwera konse ku Chiweruzo, koma wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo.” Ndizo Zamuyaya monga Mulungu Mwiniwake, chifukwa ndi Mawu Ake.

³⁹ Mulungu ndi Mulungu mmodzi. Iye sangadzisakanize Yekha ndi zinthu zina, Iye ndi wosagawanika. Mulungu ndi Mulungu. Lamulo loyamba, ndiro, “Inu musadzakhale ndi milungu yina pambuyo pa Ine.”

⁴⁰ Chotero simungasakanize mafuta ndi madzi ndi kuzipanga izo kuti zigwire bwino ntchito. Akuyenera kukhala madzi kapena mafuta. Ndipo Mulungu akadali Mulungu yemweyo. Tiri ndi chipembedzo chomwe chimasakaniza ndikuti, “Mulungu anali, nthawiyina anachitapo *ichi*, ndipo sakuchita icho lero,” ndiye tikuyesera kuyika mafuta ndi madzi pamodzi. Chifukwa, Iye. . .

⁴¹ Lemba linati, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.” Izo sizingangosakanikirana ndi kusakhulupirira; chikhulupiriro sichingatero.

⁴² Ife tiri nacho chikhulupiriro mwa Mulungu. Ndi Wamuyaya. Kusakhulupirira kwakhala kulipo, kuyambira mmunda wa Edeni. Mulungu nthawizonse wakhala akufuna kuti anthu Ake akhulupirire izi. Iye wakhala akufuna kuti iwo akhale ndi chidaliro, ndi kuti—kuti adziwonetsere Yekha pakati pa anthu Ake. Mulungu ndi Mzimu.

⁴³ Mu Yohane Woyera mutu wa 15, ndime ya 1, Yesu anati, “Ine ndi Mpesa; inu ndinu nthambi.” Tsopano, nthambi ndi Mpesa zimalumikizana pamodzi. Ndipo Mulungu nthawizonse wakhala akuyesetsa kuti awapeze anthu amene Iye angakhoze kukhalamo, kuti Iye adzathe kuwonetsera ulemelero Wake pakati pa anthu Ake.

⁴⁴ Chotero ife tikuwerenga apa kuti Davide anafuula mokweza, ndipo anati, “O Ambuye Mulungu, bwererani kwa ife kachiwiri. Ife tachimwa ndipo tatembenuka kuchoka kwa Inu. Inu Amene mumakhala pakati pa guwa ndi akerubi, walani kenanso.”

Pakuti iye ankadziwa kuti nthawi ina Iye anali Mulungu pakati pawo, ndipo Davide ankadziwa kuti Iye anali akadali Mulungu. Anthu anali atadzipatula okha kwa Iye. Mulungu sankawala kenanso. Izo sizinali chifukwa chakuti Iye samatha kuwalanso. Ndi chifukwa chakuti anthu anatsekereza chifundo Chake kwa iwo, ndi tchimo lawo. Kenako Davide akupita ku lemba lathu. Masalmo 80:7.

⁴⁵ Iye anati, “Inu munazula mpesa, kuchokera ku Igupto, ndipo munawutulutsa iwo ndi kudzaubzala iwo pamalo abwino.” Ameneyo anali Israeli, anthu a Mulungu amene anali mu Igupto. Iwo anali mpesa wabwino. Iwo anali osankhidwa a Mulungu. Koma ngati mpesa wabwino suyikidwa pa nthaka yabwino, iwo sudzabala zipatso zabwino. Zimatengera kumene mpesawo wabzalidwa, zimatsimikizira zotsatira za mbewuyo. Chotero, Mulungu anamtenga Israeli, kuchokera ku nthaka yosabereka.

⁴⁶ Ndi chinachake chonga lero. Iye tiri nawo, mdziko, okhulupirira ambiri aakulu ndi abwino, ndipo iwo asakanizikirana mmipingo yonse ya chipembedzo. Iwo achokera ku zipembedzo zosiyanasiyana ndi mayendera osiyanasiyana a moyo. Ndicho chifukwa chake, mu utumiki wanga, ine sindinayambe ndayerapo, pa nthawi iliyonse, kupondereza munthu wina aliyense kapena chipembedzo chinachake, chifukwa, mwa onsewo, muli anthu abwino. Iwo ndi oyitanidwa ndi Mulungu ndiponso anthu osankhidwa.

⁴⁷ Kodi inu mukanamuweruza Israeli pamene iye anali mu Igupto? Iwo anangoyambapo pa phazi lolakwika. Ndipo machimo awo anali atawalekanitsa iwo kwa—kwa Mulungu, ndipo iwo anakabzalidwa mu Igupto.

⁴⁸ Umo ndi momwe anthu ambiri aliri, mmipingo lero, anthu abwino angobzalidwa pamalo olakwika. Tsopano ngati wokhulupirira weniweni abweretsedwa kwa Khristu, ndipo iye nkudzabzalidwa mu chipembedzo china chachikulu chimene sichimakhulupirira mu zozizwitsa ndi zizindikiro ndi zodabwitsa za Ambuye, munthu ameneyo akhoza kukhala Mkhristu weniweni, ndi Mkatolika, Baptisti, Presbateria, Mboni za Yehova, chinachakenso. Mu mpingo umenewo, Mpesa weniweni wa Mulungu, koma kachikhulupiriro kachipembedzo kamadula Moyo wa Mpesa umenewo. Iwo sungabale chipatso Chake.

⁴⁹ Ndipo, kawirikawiri, zipatso zomwe mumazipeza kuchokera ku mpesa umene uli wopinimbira kapena umene suli mu nthaka yabwino zimakhala zipatso zoyipa. Izo zidzatulukira ngati ma apulo, ndi kudzakhala ndi mfundo ndi zodyedwa ndi mphutsi. Zimakhala zoti tizilombo tonse tibwerapo.

⁵⁰ Mpesa wabwino wathanzi suyenera kupoperedwa mankhwala. Umakhala wathanzi mokwanira kutaya adani ake onse.

⁵¹ Izo zimakhalanso chomwecho ndi Mkhristu wobadwa kachiwiri. Inu simumasowa kuti muziwapopera iwo onse nthawi zonse, ndi kuwasisita iwo pa nsana. Iwo amakhala athanzi lauzimu mokwanira kuti achotse zonyansa zonse za padziko lapansi. Iwo amakhala moyo ndi chakudya chopatsa thanzi chenicheni.

⁵² Mtengo nthawizina, umene...kapena chomera chomwe chinakhalapo mu chipululu, ndipo chinalibeko chinyezi chokwanira, icho chimadzabala chipatso chaching'ono chokhala ndi mfundo, ndipo icho sichimawoneka ngati chipatso chomwe chikuyenera kubwera kuchokera ku mpesa wake.

⁵³ M'bale wanga, mlongo, izo ndi zomwe ziri ndi mipingo lero. Wochimwa amabweramo, atatha, mwinamwake, kunyumba atatsutsika, anapita ndi kukawerenga Baibulo lake, ndipo nkupita ku tchalitchi. Mmalo mopeza maapulo okoma kapena mphesa, Moyo wa Ambuye Yesu ukuberekedwanso mu Mpingo, amakapeza malingaliro aang'ono, amfundo, odyedwa ndi mphutsi, achipembedzo, zopanda pake. "Ife Abaptisti, ife tiri nacho icho. *Iwo* alibe chochita nacho icho. Ife Amethodisti, ife tiri nacho icho." Mikono ya Mulungu imafikira kuchokera ku nyanja kupita ku nyanja, ndi kuchokera kugombe kupita kugombe, akhoza kupulumutsa mpaka kumalekezero. Koma izo ndi zimene ife timaziyeza mmalo omwe timapitako.

⁵⁴ Izo ziri monga Davide ananenanso, kenanso, mu Masalmo 1. Iye anati, "Wodala ndi munthu amene sadzayanjana ndi onyoza awa ndi anthu opanda umulungu, osalumikizana nawo, osakhala pampando ndi iwo. Inu mukudziwa, onyoza omwe amati, 'Masiku a zozizwitsa anapita. Ndipo ubatizo wa Mzimu Woyera ndi kungodzipangitsa kukhulupirira.' Wodala ndi munthu amene sadzachita zimenezo. Wodala ndi munthu amene adzaimirira kwa chinthu choterocho. Iwo safuna kusakaniza izo pamodzi. Ndipo inu simungasakanize zinthu zimenezo pamodzi. Wodala ndi munthu amene sadzadzisonkhanitsa yekha ndi kupita ku chimodzi mwa zinthu zimenezo zomwe zimakana Mphamvu ya Ambuye."

⁵⁵ Baibulo linati, "Tulukani pakati pa oterowo, pakuti tsiku lidzafika limene iwo adzakhala aliwuma, odzikuza, okonda zokondweretsa koposa kukonda Mulungu; okhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma kukana Mphamvu yake: kwa oterowo chokaniko."

⁵⁶ "Wodala ndi munthu amene sadzasonkhana limodzi ndi onyoza awa, omachita chipongwe, kumawutcha Mpingo wona, 'gulu la otengeka.' Iye adzakhala ngati mtengo wobzalidwa m'mpheapete mwa mitsinje yamadzi." Mulungu wamuyika iye pamalo oti asankhe. "Zipatso zake sizidzafota. Iye adzatulutsa masamba ake ndi zipatso mu nyengo yake." Penyani momwe Davide ananenera zimenezo. "Mwamuna

uyu ndi wodalitsika. Iye adzabzalidwa,” osati kungoyikidwa pamene. Inu mukudziwa, ndimakonda kuwona chirichonse chobzalidwa.

⁵⁷ Tsopano, Israeli, mu Igupto, sanabzalidwe. Iwo anangoyikidwako. Iko sikunali kwawo kwa pachiyambi. Ndipo munthu amene ali Mkhristu, yemwe amakhazikitsa kopita kwake Kwamuyaya pa kachikhulupiriro kena kachipembedzo, iye sali pamalo ake oyenera. Iye anabadwa kuti adzakhale mfulu, ndi mwana wa Mulungu, kuti azipembedza Mulungu. Koma iye amakhala pansu pa kachikhulupiriro, iye sangathe kubala chipatso chake, komabe chinachake mwa iye chimalakalaka kuchita icho.

⁵⁸ “Iye adzakhala ngati mtengo wobzalidwa m’mphepete mwa mitsinje ya madzi.” Mitsinje, yochuluka; madzi, amodzi. Mitsinje yambiri ikubwera mu mpita umodzi. Mwa kuyankhula kwina, iye adzakhala ngati munthu mu Lemba, amene amakhulupirira Mawu onse a Mulungu, kumene Mphamvu ndi mphatso naini za uzimu zikhoza kumayenda, kudzera mwa Mulungu mmodzi, kukalowa mkati mwake mwenimweni.

⁵⁹ Anthu samakhulupirira mu kufuula. Chinthu chake ndi chakuti, iwo alibe chisangalalo chauzimu. Ndipo zisangalalo za madzi a Moyo zikhoza kuyenderera. Ndiro gawo lonse lomwe liri vuto la Branham Tabernacle, chifukwa kusakhulupirira kumeneko, zosamalira za mdziko zinali zitawamanga anthu mpaka izo sizingakhoze kubala kukula kwauzimu.

⁶⁰ Ndiro vuto ndi dziko lathu. Ndiro vuto ndi mipingo yathu. Iwo alibe chimwenwe. Ndipo chimwenwe cha Ambuye chinachokapo. Monga kunalembedwa nthawi ina mu Lemba, mawu Achiheberi a Ikabodi, amene amatanthauza, “Kukhalapo kwa Ambuye kwachokapo.” Ndizo pa mipingo yathu, chifukwa chakuti ife tinachoka pa maziko apachiyambi, ndipo tinadziyika tokha mu tizikhulupiriro ndi chipembedzo, ndipo tinaloleza zinthu za mdziko kuti ziwumitse zotichitikira zathu ndi Mulungu.

⁶¹ Oh, mudzapite nane ku Arizona. Mundilore ine ndidzakutengereni inu ku zipululu, kumene ndayendako zaka zambiri. Chirichonse mchipululu chimakhala ndi chomata pa icho. Chomera chaching’ono chirichonse chimene mungachipeze, musachiyandikire icho, chidzakumatani inu. Nthawizonse zimakhala ndi zomata, zokonzeka kumata chirichonse chomwe chingayandikire icho. Vuto ndi chiyani? Chinapanga icho kukhala chomata ndi chiyani? Ndi chifukwa chinalibe madzi. Ndi chimene chinawumitsa icho. Chomata chimenecho ndi tsamba, lokulungidwa. Chifukwa chosowa madzi, ilo limadzakhala chomata.

⁶² Ndi momwemo ziriri ndi Mpingo, lero, kuti pamene mpingo uchoka ku Kasupe wa Moyo. Pamene uchoka ku chisangalalo

cha chipulumutso, pamene uchoka kwa Ambuye Mulungu, ndiye munthu ameneyo amadzakhala chobaya, nthawizonse amapeza cholakwika, kumabaya. Mosakhalitsa inu mumabwera, “Ndine wa Presbateria. Ndine wa Methodist. Ndine *wakuti-ndi-wakuti*. Musandiyankhule ine za zinthu zimenezo.” Chobaya! Chiribe zipatso.

⁶³ Inu mutenge chomera chomwecho, akaloga, ndikukachiyika icho mdziko kwa timbadwo tingapo, komwe kuli madzi ambiri, ndipo chobaya chimenecho chidzafutukuka ndipo padzabwera tsamba lofewa, lobala zipatso.

⁶⁴ Vuto ndi chiyani ndi mpingo lero? Iwo wakhazikitsidwa mu chipembedzo, chimene chayika tizikhulupiriro tachipembedzo ndi kuwumanga iwo, palibepo chisangalalo, kungokonkha apo ndi apo, kwa chitsitsimutso chaching’ono kuti chiwugwire iwo. Chimene chikuyenera kukhala, ndicho kutuluka pakati pa onyoza ndi osakhulupirira, ndi kudzabzalidwa mmphepete mwa mitsinje ya madzi.

Pakuti pali Kasupe wodzaza ndi Magazi,
Wotuluka kuchokera mmitsempha ya
Emanuele,
Kumene ochimwa, (osakhulupirira) akagwera
pansi pa kusefukirako,
Amataya madontho awo onse olakwa.

⁶⁵ “Mtengo,” Davide anati, “umene wabzalidwa mmphepete mwa mitsinje ya madzi.” Oh! Mulungu sangayenderera Yekha kudutsa mwa akaloga.

⁶⁶ Tsopano, madzi amayimira moyo. Ife tikudziwa kuti Mose, mu chipululu, anakantha Thanthwe, ndipo linapereka madzi a moyo kwa anthu owonongeka. Ndipo Yesu anati, “Monga Mose anakantha thanthwe mu chipululu, chomwechonso Mwana wa munthu akuyenera kukwezedwa mmwamba,” ndipo Iye anakanthidwa.

⁶⁷ Moyo umakhala mu khungu la magazi. Ndipo Moyo umenewo sungabwere mpaka khungu la Magazi litasokonezedwa ndi kuswedwa.

⁶⁸ Pamene Mulungu anatulutsa Israeli, Iye anawapatsa iwo yesero, monga fuko. Iye anawazula iwo mu Igupto, pakati pa osakhulupirira. Ndipo anadzawabweretsa iwo mu chisamaliro Chake, pa mapiko a mphungu, mphungu yaikulu ija, Mose, yemwe ankawatsogolera iwo kuchokera kumalo kupita ku malo, akuyesetsa kuti awafikitse iwo mu chikhalidwe, kuti awoloke. Kwa zaka forte Iye anawatsogolera iwo ndi kumawadyetsa iwo mu chipululu. Ndipo anaipatsa chonde nthakayo, nthaka yabwino, nthaka yosankhidwa. Ndipo Iye anawonetsera chozizwitsa Chake, zizindikiro ndi zodabwitsa, kwa zaka forte mu chipululu. Iye ankabala zozizwitsa ndi zizindikiro, mwa mneneri uyu, kuti awonetsera kuti Iye anali Mulungu.

Ndani akanawumitsa nyanja koma Iye? Ndani akanakantha Igupto koma Iye? Ndani akanayerekeza kukweza dzanja koma Iye? Koma, pakati pa izo zonse, Iye anali Mulungu, ndipo Iye anadziwonetsera Yekha Mulungu. Iye ndithudi ankafuna kuti anthu Ake azichita chomwecho.

⁶⁹ Kenako Iye ananyowetsa nthaka ya Palestina, ndi magari a mbuzi ndi ng'ombe zazikazi, ng'ombe zazimuna, nkhosa. Koma anthuwo samatha kukhazikika. Izo sizinali zokwanira, chifukwa moyo wa ng'ombe yayimuna. . . Khungu la magari limasweka, ndipo moyo wa chinyama umabwereranso, iwo sumagwirizana ndi moyo wa munthu.

⁷⁰ Tsiku lina, Mulungu anatsimikiza kuti Iye apulumutse anthu Ake, Mpingo Wake wokonzedweratu. Iye ankayenera kuti achite zimenezo, Iyemwini, chifukwa Iye anazikonzeratu izo maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe.

⁷¹ Munthu ndi wolephera, ndipo nthawizonse adzakhala. Iye ndi wolephera, kuyamba ndi kuyamba, ndipo iye nthawizonse adzakhala wolephera.

⁷² Mulungu, mu kukonzedweratu Kwake, mu malingaliro Ake Omwe aakulu opanda malire, anakonza dongosolo loyika Mpesa weniweni mnthaka. Ndipo Iye anabzala pa dziko lapansi lino, Mpesa, Mpesa wolungama; osati chipembedzo, osati mpingo, osati kachikhulupiriro, koma Munthu, Mwiniwake, atapangidwa thupi. Ndipo Iye anawonetsera mtendere Wake, Mphamvu Yake, Mngelo wamkulu wa Mulungu. Yehova wamkulu anali ndi Iye. Ndipo mwa Iye munali chidzalo cha Umulungu mu thupi. Ndipo anthu sanamukhulupirire Iye; ndipo sanamukhulupirire Iye chifukwa Iye sankagwirizana ndi tizikhulupiriro tawo.

⁷³ Pomaliza, iwo anamutengera Iye ku Kalvare. Kumeneko khungu la Magazi lija linaswedwa, la Mwana wofunikira wa Mulungu, Thupi limene Yehova ankakhalamo. Pamenepo panadzabwera Mpesa, ndi mizu Yake mu Ulemelero, ndi nthambi Zake pa dziko lapansi, kuti akapange Mpingo wa Mulungu wamoyo, umene ukanati udzawonetsere chiukitsiro Chake ndi Mphamvu Yake. Ndi ndani amuna ndi akazi awa amene akanadzawukana Mpingo umenewo, Mpesa wa Mulungu wamoyo? Zosalephera nthawizonse. . . Kukhalapo kwa Ambuye Yesu ndi Mpingo Wake, kuti adzakhale moyo, ndi kudzawonetsera nthambi Zake zokonzedweratu, amene Iye anawagwira maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Ndipo analumbira, pa iwo, kuti Iye akanadzawaukitsa iwo. Ndipo Mpingo Wake, lero, ndi ulemelero wa chiwukitsiro Chake ukukhala mwa Iye! “Ine ndi Mpesa; inu ndinu nthambi.” Nthawi zonse pamene mtima ugunda, magari amagunda kwa membala aliyense wa thupi. Nthawi iliyonse mtima wokhulupirika wa Mulungu ukagunda, iwo umagundira kudzera mu Dzina la Yesu

Khristu, kwa Mpingo, “Chirichonse chimene inu mupempha mu Dzina Langa, icho Ine ndidzachichita. Ine ndiri nanu nthawizonse, mpaka ku chimaliziro cha dziko lapansi.”

⁷⁴ Nzosadabwitsa Petro ananena, pa Tsiku la Pentekoste, “Lapani, aliyense wa inu, mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu, ndipo inu mudzazazidwa ndi Moyo wochokera ku Mpesa.” Mzimu Woyera ukupereka Dzina Lake, zimenezo, ngati ife tiri olumikizana ndi Iye. Iye ndi wolumikizana ndi Mulungu, chifukwa Iye anali Muzu ndi Mphukira ya Mulungu.

⁷⁵ Iye anabwera kudziko lapansi. “Dziko lapansi linapangidwa ndi Iye. Iye anabwera ku dziko lapansi; ndipo dziko silinamudziwe Iye.”

⁷⁶ Ndipo tsopano, lero, Iye, kufa Kwake kutachitika, kuti adzapereke khungu la Magazi, kuti lidzaswedwe, kuti kupyolera mu Magazi a Yesu Khristu Mpingo udzakhoze kuyeretsedwa ndi kuyikidwa mu dongosolo. Kuti, Mzimu Woyera wawukulu, umene uli Moyo wa Mpesa, Moyo Wamuyaya wa Mpesa, Mzimu Woyera umenewo udzakhoze kumagunda mwa membala aliyense wa Mpingo wa Mulungu wamoyo.

⁷⁷ Nzosadabwitsa kuti iwo ndi anthu osamvetseka komanso achilendo. Nzosadabwitsa iwo amachita mwachilendo. Iwo alibenso zochita za dziko lino, pakuti iwo ndi akufa ndipo anayikidwa mmanda mwa Khristu, ndipo anawukira ku moyo watso, kuti adzakhale zipatso zoyamba za iwo amene amakondwera ndi chiukitsiro chazimu, kuti Mzimu Woyera udzapite kudutsa mwa membala aliyense, ndi kudzasonyezera ulemelero wa Mulungu, monga Mulungu anawonetsera Igupto pamene Iye ankabala Mpesa.

⁷⁸ Tsopano, ulipo mpesa wakuthengo. Baibulo limanena za iwo mu Mafumu Achiwiri. Ndipo kodi inu munazindikira, pamene mlaliki uyu anapita kukathyola nandolo, iye anakachoka pa mpesa wakuthengo. Mipesa yakuthengo imeneyo ikuyenera kuti imamera pafupi ndi seminare kwinakwake, chifukwa kunali ku sukulu ya aneneri. Ndipo anatenga mphonda zodzaza pachilolo. Iye anaziponyera izo mu ketulo, ndipo ankayesera kuti azisakanize izo ndi zenizeni, chipere chenicheni. Ndipo iwo anafuula, “Muli imfa mu mphikamo.”

⁷⁹ M’bale, pali mpesa wakuthengo umene wamera, ndipo iwo wamera mozungulira kachikhulupiriro, chipembedzo. Ndipo pamene iwo ufika kunja uko, iwo umatsekereza chimwemwe chonse chazimu. Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, mpesa umenewo ndi wakufa.

⁸⁰ Koma Mulungu watsimikiza kuti mpesa Wake sudzafa. Kotero Iye anawudzula Iwo, kuchokera mu tizikhulupiriro timeneto, ndipo anawudzaza Iwo ndi Mzimu Woyera, ndi kudzawubzala Iwo pansu, mu Dzina la Yesu Khristu. Pamenepo

Mpingo umenewo ukhoza kumagunda ndi kukhala moyo, ndi kumasangalala, kumamverera Kukhalapo kwa Mulungu wamoyo, kumamuwona Iye akuyenda ndi kumachita zinthu zomwe Iye anachita pamene Iye anali pano pa dziko lapansi.

⁸¹ Chifukwa chiyani? Nthambi Zake, chilumikizo Chake, muzu Wake, chiyambi Chake, chinali Mulungu. Iye anali Mwanawankhosa wophedwa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Pasanakhale konse dziko lapansi, Iye anali ndi Mulungu. Iye anali Muzu ndi Mphukira ya Davide, Nyenyezi ya Mmawa, Kakombo wa Mchigwa. Zimenezo Iye anali.

⁸² Mizu yake inakulungidwa momuzungulira Mulungu, mozungulira Mpandowachifumu, mozungulira Ufumu wa Mulungu. Mizu yake inakulungidwa. Moyo Wake umafalikira padziko lapansi. Ndipo Iye anapereka Moyo Wake, kuti Iye adzathe kubwerera ku mizu ndi kukagundanso kachiwiri, kukabala nthambi kuchokera mu Mpesa umenewo, umene uli Mpingo Wake ukuwonetsera zotsatira zomwezo zimene Iye anachita pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, kuti amupange Iye yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

⁸³ O Mpingo wa Mulungu wamoyo, khulupirani izi, Choonadi! Ndi Uyo apo. Pamene Mzimu wooka wa Mulungu usunthira pa wokhulupirira, chirichonse chimene Lemba likunena, iye amati, “Ameni.” Chifukwa chiyani? Ndi Mzimu Woyera umene unalemba Baibulo, uli mwa iye, ukugunda moyo wake. Iye samasamala yemwe wakhala pozungulira, kapena chimene wina aliyense akunena. Izo nthawizonse zimagwirizana ndi Mawu.

⁸⁴ Pali zabodza. Ndi mphonda. Zochokera ku mpesa wakuthengo. Ndi mpesa waukulu, waphimba dziko lonse, koma iyo ndi imfa. Zambiri zomwe zaponyedwa pakati pa anthu.

⁸⁵ Koma, kumbukirani, “Chakudya” chimabweretsa iwo ku Moyo, kuwudzula iwo ndi kuwuyika iwo pa malo abwino, amene ali Khristu Yesu. Chirichonse chimene Mawu Ake ali, mulole Iwo akhale “ameni,” kwa inu. Ndiye Mzimu wa Mulungu, ndiye, chisangalalo chauzimu chidzayenda ngati mtsinje. “Iye adzakhala ngati munthu, mtengo, wobzalidwa m’mphepete mwa mitsinje ya madzi. Masamba ake sadzafota. Iye sadzakhala pampando wa onyoza kapena osakhulupirira, kapena munthu wopanda umulungu yemwe amakhala motsatira zinthu za mdziko, koma iye adzabala zipatso mu nyengo yake.” Chipatso cha mtundu wanji? Ngati munabzalidwa mwa Khristu, mudzabala zipatso zauzimu, zipatso zauzimu za Mzimu Woyera. Mzimu Woyera umakhala moyo mwa inu.

⁸⁶ Izo zinalankhulidwa bwino, ndi mkazi pa chitsime. Potseka, tinganene ichi. Iye anati, pamene iye anamuwona Iye, Iye

ankawoneka ngati munthu wamba. Panalibe kalikonse kamene kanali kokayikitsa za Iwo, mawonekedwe, kani.

⁸⁷ Pakuti Lemba linati, “Palibe kukongola komwe tikuyenera kumukhumbira Iye. Tinabisa nkhope zathu kwa Iye.”

⁸⁸ Ndipo iwo akuchita chinthu chomwecho lero. Ngati iwo sakuchita bwino ndi zipatso zauzimu za Mzimu, ngati iwo sakuchita bwino pa zinthu za Mulungu, Khristu amakhala chinthu chonyansa kwa iwo, “Gulu la oyera odzigudubuza, gulu la anthu openga omwe alibe malingaliro abwino.”

⁸⁹ Koma, kwa wokhulupirira, iye amawakumbatira Iwo. Iwo ndi Moyo Wamuyaya. Palibe chimene chingatilekanitse ndi chikondi cha Mulungu. Ngakhale imfa, kapena chisoni, kapena njala, kapena chirichonse sichingatilekanitse ife. Ndife otetezedwa Kwamuyaya mu zomangira Zake. Ndi ife apo, pamene iye akukumbatira mtanda umenewo.

⁹⁰ Mkaziyo anati, pamene...Iye anafunsa funso, “Kodi ungandibweretsere Ine akumwa?”

⁹¹ Iye anati, “Koma si mwambo kuti Inu, mwamuna, Myuda, mumufunse Msamariya, inemwini, funso loterolo.”

⁹² Iye anati, “Koma iwe ukanadziwa...” Mwakuyankhula kwina, monga chonchi, “Ngati iwe ukanadziwa kuti uli pafupi bwanji ndi Kasupe wa Moyo, Ine ndikanakupatsa madzi oti sukanadzabweranso kuno kudzatunga. Ine ndidzakuwokera iwe, Msamariya iwe. Ine ndidzakubweretsa iwe, iwe wochimwa.” Ameneyo ndi wosakhulupirira, ndipo samakhulupirira mwa Iwo. “Ngati utangondilola Ine kuti ndikuzule iwe mmawa uno, Iye anati, Ine ndidzakubzala iwe mmphepete mwa mitsinje ya madzi. Ine ndidzakuyika iwe pamalo, mwa ubatizo wa Mzimu Woyera, mwakuti udzakhulupirira Mawu aliwonse amene Ine ndikunena kuti ndi Choonadi. Iwe udzangondilola Ine ndikuzule iwe, mmawa uno, iwe udzakhala nthambi yabwino. Iwe si wa m'munda wampesa wam'tchirewo. Iwe ndi wa *kuno*, chotero undirole Ine ndikuzule iwe; ndikubzala iwe mu Dzina Langa, mmphepete mwa mitsinje, gawo lililonse la Mawu a Mulungu. Pakuti Mawu aliwonse a Mulungu ndi owona. Lonjezo lililonse Lauzimu ndi Choonadi. Ndidzakubzala iwe pa mitsinje ya madzi amodzi, Mulungu mmodzi. Ndipo iwe udzabala zipatso, mu nyengo yako. Masamba ako sadzafota. Ndipo chirichonse chimene uchita chidzapambana. Udzayima pamene palibe malo ena oti uyimepo. Iwe udzayima, mulimonse, podziwa kuti Mulungu anapanga lonjezo. Undirole Ine ndikuzule iwe,” Iye anati, “ndi kudzakubzala iwe kuno pafupi ndi Madzi awa, kuti iwe—usadzathamangire ku malo atizikhulupiriro awa, ndi malo achipembedzo, kuti ukapezeko. Iwe sukapezako Iwo kumeneko, mulimonse. Undirole Ine ndikuzule iwe, pa chitsime chakale chowuma ichi apa, chimene umachita kutenga zidebe za malata, ndi kuphokosera ndi kukangana, ndi kumwa pang'ono,

ndi kubwerera ndi kudzamwa pang'ono. Ine ndidzakupatsa iwe Moyo Wamuyaya, chisangalalo, monga ngati chitsime, chotumphukira ku Moyo wosatha. Undirole Ine. Undirole Ine ndikuchitire iwe zimenezo,” Khristu anatero kwa mkazi, wochimwa.

⁹³ Ndipo Iye akunena chinthu chomwecho kwa Mpingo mmawa uno. Inu mukudziwa kuti kuli Mulungu. Mumakhulupirira kuti alipo Mulungu. Koma mu mgwirizano wanu, chinachake chikukudulani inu. Inu muli mchipululu. Mulibemo chisangalalo chاوزimu. Mukufuna kumverera monga anachitira pa Tsiku la Pentekoste. Kodi simungakonde kukhala ndi chisangalalo chomwe iwo anali nacho?

⁹⁴ Pamene Mulungu anatsanulira mu Moyo Wake, mu nthambi yoyamba ya mtengo, mtengo umenewo unayamba kuchita ngati anthu oledzera. Iwo anadzandima pansi pa mphamvu ya Mzimu. Akazi okondeka, aang'ono oyera monga namwali Mariya, kunja uko akuchita ngati oledzera. Oh, iye anali ataledzera Mzimu. Ndipo iye anayesera kuyankhula, ndipo iye sanathe. Iye anali ndi *milomo yachibwibwi*, zimene zikutanthauza “ogawanika,” ndiko kuchita chibwibwi, kuyesera kuti anene chinachake. Iye anali wodzazidwa kwambiri ndi Mzimu, iye sakanakhoza kunena izo. “Uh-uh-uh-uh,” milomo yachibwibwi. Kenako, mwadzidzidzi, ndi chinenero china, iwo anayankhula momveka.

⁹⁵ Ndipo mlaliki wamng'ono yemwe sankadziwa mokwanira kuti alembe dzina lake lomwe pa chidutswa cha pepala, anatembenuza bokosi la sopo kapena chinachake, kapena chitsa, ndipo analumphira pa icho.

⁹⁶ Chabwino, osakhulupirira amenewo anayamba kunena, “Amuna awa aledzera. Limenelo ndi gulu lija la oyera odzigudubuza.”

⁹⁷ Munthu wamng'ono uyu anatenga Lemba; osati bukhu la kachikhulupiriro, koma Lemba. Anati, “Inu amuna a Israeli, ndi inu okhala mu Yerusalemu, ichi chidziwike kwa inu. Pakuti awa sanaledzere monga inu mukuganizira, popeza ndi ora lachitatu la tsiku. Koma ichi ndi *chija* chimene chinanenedwa ndi mneneri Yoweli, ‘Izo zidzachitika mmasiku otsiriza, atero Mulungu, Ine ndidzatsanulira Mzimu Wanga,’ ndicho chimene chikuwafufumitsa iwo.”

⁹⁸ Kodi inu mungafune kuti muzulidwe kuchoka ku kachikhulupiriro kakale ka mtundu wina, ndi kudzakhazikitsidwa pa a Kasupe a Moyo, kumene kuli mtendere ngati mtsinje?

⁹⁹ Imfa, payokha, kwa mnyamata wamng'ono wayima apoyo, wodzazidwa ndi khansa, koma walandira Mzimu Woyera. Ndipo madokotala amuuzwa iye kuti akufa. Abambo ake anamufunsa iye, “Kodi—iwe ukuchita mantha?”

¹⁰⁰ Iye anati, “Ndine wokonzeka. Ndine wokonzeka. Ndipo kuti ndisiye umboni kwa dziko lino, mudzandiike ine mu zofiira, pakuti icho chidzakhala chizindikiro kuti Magazi a Yesu Khristu anandiphimba ine.”

¹⁰¹ Icho ndi chimene Iwo amachita. Chisangalalo, ngati mtsinje, kukhoza kuyenda pamaso pa imfa, kuyenda pamaso pa dziko lapansi, kuyenda pamaso pa mayesero, kuyima pamaso pa otsutsa ndi kuwala ngati Mngelo. Chifukwa chiyani? Moyo wanu si wanu wanu. Inu ndinu wakufa, ndipo inu munayikidwa mmanda mu Dzina la Yesu Khristu, ndi kuwukitsidwa kachiwiri ku Moyo watsopano. Iye akhoza kugunda kupyolera mwa inu, mdalitso Wake, ndi kubala nthambi zomwe zalumikizidwa ndi Mpesa. “Ndidzawayika iwo pamalo osankhika.” Mulungu anati Mwana Wake anali kusankha Kwake.

¹⁰² Kodi mumalowa bwanji mwa Khristu? Kodi Petro ananena chiyani pa Tsiku la Pentekoste, momwe tingalowere mwa Khristu? Iye anati, “Lapani, aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu, kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu, ndipo mudzalandira mphantho ya Mzimu Woyera. Pakuti lonjezo liri kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa iwo amene ali kutali, ngakhale onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawayitana.” Zimenezo zikuphatikizapo inu, kuyitanako. “Lapani, batizidwani mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha tchimo lanu. Lonjezo liri kwa inu.”

¹⁰³ Oh, m’bale, Mzimu woona wa Mulungu udzagunda pa Iwo, ndikuti, “Icho ndi Choonadi.” Taonani mphonda zimenezo ndi mpesa wakuthengo. Koma Mzimu woona wa Mulungu, umene ukufuna kuti uzabzalidwe pa malo osankhidwa, kumene kuli zipatso za Mzimu.

¹⁰⁴ Ndipo kodi Yesu anachita chiyani ndiye? Iye anati, “Pokhala kuti mkazi ameneyo akufuna kuvomereza zimenezo . . .”

Iye anati, “Ambuye, ndipatseni ine Madzi amenewo. Ine ndikufuna Madzi amenewo.”

¹⁰⁵ Anati, “Siya mmphika wako wakale pamenepo. Iwe susowanso mtsuku wamadzi wamtundu umenewo. Iwe susowanso kalata yako ku kachikhulupiriro kako. Usiye njira yako yakachitidwe kako ka Presbateria, Baptisti, Methodisti, Pentekoste, zisiye mmbuyo. Bwera ku Kasupe kuno. Ndipo Ine ndidzakudzaza iwe ndi chisangalalo chomwe chidzayenderere ngati mtsinje.”

¹⁰⁶ Monga momwe adanenera wakuda wakale, “Ine ndiri ndi mtendere ngati mtsinje.” Umayenderera usana ndi usiku. Pamaso pa imfa, iwo umayenderera chimodzimodzi basi.

¹⁰⁷ Paulo anati, “Imfa mbola yako ili kuti? Ndipo manda chigonjetso chako chiri kuti? Koma ayamikike Mulungu amene amatipatsa ife chigonjetso kudzera mwa Yesu Khristu.” Ndithudi.

108 Iye anayang'ana pa Iye. Iye anayamba kuyankhula ndi Iye za malo opembedzera. Ndipo Iye anati kwa iye, “Pita ukamutenge mwamuna wako.” (“Ndimumdziwitsa iye ngati Mulungu akadali moyo. Ndine Mpesa.”) “Pita ukamutenge mwamuna wako.”

“Chifukwa chiyani,” iye anati, “Ine ndiribe mwamuna aliyense.”

109 Iye anati, “Uko nkulondola. Iwe uli nawo asanu, ndipo amene ukukhala naye tsopano si mwamuna wako.”

110 Iye anapotoloka. Chinali chiyani icho? Kwake—komezanitsidwa kwake, moyo wa moyo wake, kumene iye anali atazulidwako ku mtengo wakale wa kachikhulupiriro uwu, unali utamugwirako, pamene kugunda koyamba kwa Mulungu kunadza mu nthambi zake.

111 “Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndinu mneneri. Ndipo ine ndikudziwa Lemba linati Mesiya adzabwera ndipo Iye adzachita chinthu ichi.”

Iye anati, “Ine ndi Iye. Ine ndi Iye.”

112 Iye anasiya kachikhulupiriro kakale kaja kali pamenepo. Mwamphamvu momwe iye akanapitira, iye anayamba kumwaza nkhaniyo. “Bwerani, mudzamuwone Munthu Amene wandiuza ine zinthu zimene ine ndazichita. Kodi Uyu si Mesiya yemweyo? Mesiya ndi Mulungu wodzozedwa. Anamuzindikira Iye ngati Mulungu, Emanuele mneneri, Mulungu.

“Ine ndine Mpesa. Inu ndinu nthambi.”

113 Iye anati, “Chabwino, anthu inu, Ayuda inu mumalambira ku Yerusalemu. Inu muli ndi mpingo waukulu kumeneko, ndi kachikhulupiriro.”

Iye anati, “Ine ndikudziwa zimenezo.”

Iye anati, “Ife timapembedza mu phiri ili apa.”

114 Iye anati, “Ine ndikudziwa zimenezo. Koma nthawi ikudza, ndipo tsopano ilipo, pamene tizikhulupiriro ta ku Yerusalemu timeneto, kapena kachikhulupiriro ka Chisamariya aka, sikadzagwira ntchito. Pakuti Mulungu ndi Mzimu, ndipo iwo amene amamupembedza Iye akuyenera kumupembedza Iye mu Mzimu ndi mu Choonadi.”

115 Imeneyo ndi nthambi imene ikugwira Choonadi. “Lapani, aliyense wa inu, mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha tchimo lanu,” ndipo mudzalumikizana ndi nthambi. Inu mudzakhala ndi izi, chinthu chomwecho, pakuti Mzimu wa Mulungu udzagunda mwa inu, udzabweretsa kwa inu, mitsinje ya chisangalalo, mtendere, kuleza mtima, chikhulupiriro, ubwino, chifatso, kudekha. Udzakupatsani inu, kudzapanga kuchokera ku a . . . Kuchokera ku nkhandwe, iwo udzapanga mwanawankhosa kuchokera mwa inu. Kuchokera ku khwangwala, udzakupangani kukhala

nkhunda. Mukuona? Ndi Mzimu wa Mulungu wamoyo umene umasintha chikhalidwe chanu. Tsopano bwerani mwa Iye, ndipo mudzamedzanitsidwemo ndipo mudzakhale imodzi ya nthambi Zake. Kwa tsiku limodzi . . .

¹¹⁶ Mzere wa Moyo umenewo umene wayikidwa pansi monga chonchi, ndi Moyo wa Khristu, Mzimu Woyera, wolumikizidwa ndi Ufumu wa Mulungu. Mulungu adzatsitsira pansi nthambi Yamuyaya ija, tsiku lina, ndipo iwo onse amene anafa mwa Khristu Iye adzawabweretsa limodzi ndi Iye, pamene Iye adzawukwezera mmwamba Mtengowo kachiwiri. Umene unabzalidwa mmphepete mwa mitsinje ya Moyo, kumene Mtengo wobiriwira nthawizonse sufota kapena kutaya masamba Ake.

¹¹⁷ Pamene Iwo ukufikira pa nthambi kwa inu mmawa uno, mzanga wokonedwa, ulandire Iwo, ndipo uzulidwe ku tchimo lako, uzulidwe ku kukayikira kwako, kuchokera ku kachikhulupiriro kako.

¹¹⁸ Ine sindikukuuzani inu kuti musiye tchalitchi chanu. Inu mukhale ndi tchalitchi chanu, koma mubwere kwa Khristu. Ndi zimenezotu. Ine sindikusamala kuti mumapita ku tchalitchi chiti, bola ngati inu mungabwere ku Kasupe ameneyo amene ali wodzazidwa ndi Magazi.

¹¹⁹ Landirani Moyo Wake, ndipo mulole Iwo ukukwezeni inu, ukukwezeni inu kuchokera ku chisiro cha mdziko, mpaka zinthu zonse za mdziko zitafa. “Iye amene akonda dziko, kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri nkomwe mwa iye.” Inu simungayike moyo wa dzungu mu mpesa wamphesa, ndi kubalamo mphesa. Mukuona? Ngati muli wa Khristu, inu mumakonda zinthu za Khristu. Ndinu wodzazidwa ndi Mzimu. Inu muli . . . Iye ndi Mpesa; inu ndinu nthambi. Muloleni Iye akulandireni inu mmawa uno, monga Iye anachitira ndi mkazi waku Samariya, ndipo kudzayika moyo wanu mu Moyo Wake, ndi kudzakupangani inu cholengedwa chatsopano.

Pamene ife tikuweramitsa mitu yathu mphindi yokha.

¹²⁰ Pemphero lisanabwere, kodi pangakhale ena amene angakweze dzanja lawo, akuti, “Ndipemphereni ine, m’bale. Ndikufuna kuti ndilumikizidwe kwambiri mwa Khristu.” Mulungu adalitse mtima wanu. Oh, izo nzodabwitsa. “Ndikufuna kulumikizidwa, mwa Khristu, kuti moyo wanga uzimuwalira Iye. Ndichotsenipo ine mu (anga) mantha anga onse, ndi kukaikira, ndi zokhumudwitsa, ndi tizikhulupiriro. Ndipo mundibzale ine mwa Iye, mmawa uno, kumene ndingathe kukhala ndi mtendere ngati mtsinje. Ndine wamanjenje kwambiri. Ine sindikudziwa komwe ndikupita. Ine sindikudziwa kuti ndingayime bwanji. Ndiyikeni ine pamenepo.”

¹²¹ Tsopano pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa, inu amene mungathe, amene munakweza manja anu, kodi inu

mungaima pa mapazi anu, kwa mawu chabe a pemphero? Basi...Ife tikupemphererani inu, pomwe inu mwakhalapo. Chifukwa, ife tiri...Imirirani pa mapazi anu tsopano, kuti tikhoze kupemphera.

¹²² [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi]. . . kuchotsa kwa iwo, zokhumudwitsa zonse. [Malo osajambulidwa pa tepi]. . . kuyanjana ndi opanda umulungu ake; kuyenda mu Kuwala kwatsopano, kuyambira lero mpakana. Perekani izi, Ambuye.

¹²³ Inu munati, “Pemphani, ndipo mudzalandira. Funani, ndipo mudzapeza. Gogodani, ndipo chidzatsegulidwa kwa inu.” Tsopano iwo akugogoda. Ine ndikupempha. Mulole iwo alandire izo, Ambuye. Mulole tsiku lino lisinthe miyoyo yawo mwanjira yoteroyo, mpaka pasadzakhale kukaikira kwina mmalingaliro awo. Ndipo mulole iwo adzabwere Kwawo kwa Inu, mu Tsiku limenelo.

¹²⁴ Iwo ayimirira, Ambuye, mmawa uno. Iwo akukuimirirani Inu tsopano, pamaso pa mwamuna mzawoyo. Inu munati, “Iye amene adzachite chinthu choterocho, Ine ndidzamuimira iye pamaso pa Mulungu ndi Angelo oyera. Koma ngati iye adzachita manyazi ndi Ine, ndiye, pa Tsiku limenelo, Ine ndidzachita naye manyazi.” Ambuye, iwo sakuchita manyazi, mmawa uno. Iwo ayima. Tsopano, Inu mumasunga Mawu Anu. Adzazeni iwo ndi Mzimu Wanu, ndipo apatseni iwo moyo wotumikira, kuti, mu dziko lirinkudza, iwo adzakhoze kusangalala ndi Kukhalapo kosalephera kwa Ambuye Yesu. Kuyambira lero, mpakana, ife tikuwapereka iwo kwa Inu, mu Dzina la Yesu. Amen.

¹²⁵ Mulungu akudalitseni inu. Wina pafupi ndi iwo gwirani chanza chawo, amene ali pafupi nawo.

Alipo Kasupe . . .

¹²⁶ Tsopano uthenga watha, tsopano mpembedzeni Ambuye, mungokhala ngati mwatseka maso anu.

. . . Magazi,
Kuchokera kwa Emmanuele . . . (Ameneyo
anali Mulungu, Emmanuele.)
Ndipo ochimwa, (osakhulupirira)
akagwetsedwamo . . .

Fulumirani, thamangani, kazibwerani.

. . . pansi . . .
Ataya madontho awo onse a kulakwa.
Ataya . . .

¹²⁷ Mungomupembadza Iye tsopano mu Mzimu. Mungolola mtima wanu umasuke. Ine sindikusamala kuti ndinu a mpingo wanji. Basi, mumtima mwanu, “Zikomo Inu, Mulungu wokondedwa.”

Ndipo ochimwa . . . pansi pa kusefukirako,

. . . zolakwa zawo . . .

¹²⁸ Tsopano ine ndikufuna kuti inu mukweze dzanja lanu, inu Akhristu, tsopano, okhulupirira, ndipo muyimbe iyi ndi ine.

Chiyambireni mwa chikhulupiriro ndinawona
mtsizewo

Mabala Anu owukha akupereka,

Osati kachikhulupiriro tsopano, kumbukirani.

Chikondi chowombola chakhala mutu wanga,

Ndipo chidzakhhalapo mpaka ine nditafa.

Ndipo chidzakhhalapo mpaka ine nditafa,

Ndipo chidza . . . (Icho chidzakhala
changa . . .) . . . ine nditafa;

Chowombola . . . (Osati wonyoza, koma
chikondi chowombola.) . . . chakhala mutu
wanga,

Ndipo chidzakhala mpaka ine nditafa.

¹²⁹ Inu mukutanthauza izo, kwa Iye? Nenani, “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Zikhale chomwecho. *Chikhulupiriro Changa Chikuyang’ana Kwa Inu.*

¹³⁰ Ndi angati amene akudwala ndi osowa, mmawa uno? Pambuyo pa zauzimu, umafunikira chithandizo chakuthupi. Kwezani dzanja lanu, kuti ife tikhoze kukuwonani inu. “Ndine wosowa, M’bale Branham. Ndine—ndine pano. Ine ndikudwala. Ine—ine ndikulephera kukhala bwino. Ine ndayesetsa. Ndapitapo kwa adokotala. Ine ndachitapo zonse zomwe ine ndimadziwa kuti ndichite, koma basi ine ndikulephera kuti ndipange zimenezo, izo zikuwoneka chomwecho. Koma ine ndikukhulupirira kuti Mulungu andichiritsa ine.” Inu mukukhulupirira zimenezo? Limenero ndi lonjezo Lake.

¹³¹ Tsopano, kodi inu munabzalidwa mmphete mwa mitsinje ya Madzi? Madzi ake Ati? Khristu wokanthidwa uja; kuti, monga kuchoka mu thanthwe munatuluka madzi, kudzapulumutsa anthu owonongeka ku imfa. Khristu anakanthidwa, ndipo kuchokera mu thupi Lake munatuluka Mzimu Woyera, kuti anthu owonongeka asafe koma akhale ndi Moyo Wamuyaya. Kodi inu . . . Pali zinthu zambiri zosiyana.

¹³² Mulungu amalonjeza kuti adzachiritsa. “Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, anatunduzidwa chifukwa cha kusaeruzika kwathu; chilango cha mtendere wathu chinali pa Iye; ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Mitsinje, mitsinje ya Madzi amodzi, Mzimu Woyera.

¹³³ “Pali, poyamba, atumwi, aneneri, aphunzitsi, avangeri, abusa,” mitsinje ya Madzi amodzi.

¹³⁴ “Ziripo mphatso zosiyanasiyana. Ena amayitanidwa kudzanenera. Ena amaitanidwa, kudzapereka mphatso ya machiritso. Ena ali ndi nzeru. Ena ali ndi chidziwitso, mwa

Mzimu womwewo. Ena amayankhula ndi malirime. Ena amatanthauzira. Onse mwa Mzimu womwewo,” Akorinto Woyamba 12. Ndi chiyani chimenecho? Mitsinje, mitsinje ya madzi ambiri, madzi ambiri.

¹³⁵ Mitsinje yambiri ya Madzi amodzi, Mzimu Woyera ukupereka mphatso zambiri ndi madalitso ochokera kulikonse. Iye amabweretsa mphatso zamtengo wapatali, nayenso, mphatso za machiritso, mphatso za chipulumutso, mphatso za Mzimu Woyera kuti zidzagwire ntchito mu mpingo wanu ndi pakati pa anthu. Mitsinje! Ndi chisangalalo ngati mtsinje ndi masika. Ndi zokongola bwanji!

Chikhulupiriro changa chikuyang’ana kwa
Inu,
Inu Mwanawankhosa wa Kalvare,
Mpulumutsi Waumulungu;
Tsopano ndimveni pamene ndikupemphera,
Chotsani machimo anga onse,
Oh mudirole ine kuyambira lero
Ndikhale kwathunthu. . .

¹³⁶ Tsopano, Ambuye, limenelo ndiro pemphero lathu. Ife sitikhala muchangu. Ili ndi sabata. Ili ndi tsiku limene Inu munalipanga. Ife tikuyenera kukupembedzani Inu tsiku lonse. “Tsiku lonse ndi usiku wonse,” wandakatulo anati, “Angelo amandiyang’anira ine.” Tsopano ife tikumverera kuti Iwo ali pafupi.

¹³⁷ Atate Mulungu, ine ndayankhula chinthu cholimba kwambiri. Koma ine sindinachite izo. . . Ufufuzeni mtima wanga, Ambuye. Ngati ndinachita izo mwanjiru, ndiye mundikhululukire ine. Koma ine ndinazichita izo kudzera mu chikondi kwa nthambi Yanu, Mpesa Wanu. Ine ndikupemphera, Ambuye, kuti ngati pangakhale ena pano amene ali ogwirizana mu zipembedzo zazikulu, kumbukirani. . . Ine sindikuyesera kuwafunsa iwo kuti abwere kuchokera pamenepo. Ine ndikungowapempha iwo kuti asamangidwe ndi chikhulupiriro chawo, koma kuti abwere kwa Inu, ndi kudzamasulidwa ndi kulimidwa, ndipo Mzimu utsanulidwemo. Akatero mpingo wawo udzakhala mpingo wabwinoko, mpingo wauzimu, umene Inu mukuwudzera, wopanda banga kapena wopanda khwinya, wotsukidwa Mmagazi a Mwanawankhosa. Dziko laluntha ili, lero, Atate, lafika kutali ndi izo. Iwo akufunafuna magulu aakulu ndi mipingo yayikulu, monga mpesa wakuthengo. Koma, Ambuye, ife—ife tamamatira ku chipatso chokoma chija, chipatso chija cha Mzimu, chimene chimabweretsa kukoma ku moyo wathu.

¹³⁸ Ife tikupempha tsopano kuti Inu muwadalitse anthu odwala awa amene akubwera patsogolo kuti adzapemphereredwe. Ambuye, kodi ine ndingakufunsemi Inu kamodzinsu, kodi

Inu mungayeretse nthambi yosayenera iyi, ndi Magazi Anu? Kuti Mzimu Wanu utsanulire kudzera mwa iyo, kuwonetsera Mulungu wamoyo, kuti Ndinu Mulungu yemweyo amene anayankhula kwa mkazi pa chitsime. Mulole zikhale chomwecho, kuti anthu akhale atadutsa kusokonekera, kuti iwo akakhoze kuwona kumene Mzimu wa Mulungu ukugona, uli mu mtima wa wokhulupirira, osati mu mpingo wina, koma mu mtima wa wokhulupirira. Perekani izi, Atate. Ine ndidikirira pa Inu tsopano, kuti Inu mudziwonetsere Nokha, monga Inu munawonetsera mmasiku akale. Monga munadziwonetsera Nokha kudzera mwa Yesu, Amene anafa kuti ife tidzakhale oyera, kuti Mzimu womwewo umene unkakhala mwa Iye udzakhoze kubwera kudzera mwa ife, kubweretsamo zotsatira zomwezo. Perekani izi, Atate. Pakuti ine ndikupereka zinthu zonse kwa Inu, mu Dzina lokondeka la Mwana Wanu, Yesu. Ameni.

Musandirole ine ndisochere
Kuchokera ku mbali Yanu.

¹³⁹ Chabwino, Teddy, *Kungo Khulupirira*. Tsopano ndi angati muno ali . . . ? Billy anati iye anapereka makadi ena apemphero.

¹⁴⁰ Tsopano ife takhala tiri, mu tchalitchi, pokhala kuti mwadzadza, kungotenga ndi kupempha onse omwe ndi alendo pakati pathu kuti aimirire, ndi kulola Mzimu Woyera utuluke kudzera mwa anthu amenewo ndi kuwazindikira iwo monga choncho. Ife tachitapo izo, nthawi zambiri. Tsopano, masabata angapo apitawo, winawake anati, “Koma ndi zovuta kuti anthu aziganiza choncho. Koma iwo akufuna mzere wa pemphero.” Chotero ife . . . Ndi angati anakhalapo pano pamene Mzimu Woyera umapita pa chigulu ndi kumutenga munthu aliyense kuchokera pa gululo? Ndithudi.

¹⁴¹ Tsopano, ine ndinamuza Billy kuti apereke makadi ena, kuti ife tikhoze kuyitana, mwa magulu, ndi kuwapempherera iwo, mwaona, kuti titsirizitse izo.

¹⁴² Chotero ndiye, ndipo nthawi yomweyo zikatha izi, iwo akhala ndi utumiki wa ubatizo kwa inu amene mukufuna kuti mubatizidwe. Ife tikupatsani inu malo, nthawi, mu maminiti pang’ono chabe.

¹⁴³ Choyamba, tayankhula za izi. Ife tayankhula za Mpesa uwu, cholowa ichi cha Mulungu. Tsopano, ngati izo ziri zoon, ndiye ngati ife tiri moonadi nthambi yokonzedweratu ku Mpesa umenewo, ndiye Mzimu Woyera womwewo ukuyenera kubwera kudzera mwa ife. Ndipo ngati Iwo utero, Iwo udzachita chinthu chomwecho chimene Iwo unachita kudzera mwa Iye, pakuti Iye ali Mpesa. Ife ndi nthambi. Ndipo ngati . . . Moyo umene uli mu mpesa ukuyenera kukhala mu nthambi, kuti upangitse nthambi kukhala moyo. Ngati iwo ubala zosiyana ndi chimene Mpesa uwo unabala, ndiye umenewo ndi mpesa wolakwika. Izo ndi zomwe

ndikuyesera kuti ndinene. Iwo ukuyenera kukhala Moyo womwe womwewo.

¹⁴⁴ Tsopano, ndi ndani ali ndi makadi apemphero? Kwezani mmwamba dzanja lanu!...?....Chabwino. Izo zikuyambira pati, kuyambira wani mpaka fifite, kapena wani mpaka handiredede? Kapena, ndi angati akudziwa? Ndi—ndi makadi apemphero tisanati...Dikirani. Tsopano, ndani ali ndi nambala wani? Kodi liripo khadi la pemphero nambala wani muno? Kodi liripo? Chabwino, kodi ilo layambira pati, ndiye, fifite? [M'bale akuti, "Wani kudutsa mpaka fifite."—Mkonzi]. Oh, oh, apa, wani mpaka fifite. Chabwino.

Dzaimeni pomwe apo, mwaona, nambala wani.

Nambala thuu. Nambala thuu. Chabwino, dzaimeni pomwe apo.

¹⁴⁵ Nambala firii, khadi la pemphero nambala firii. Kodi liripo mchipinda muno? Kodi iwo angaimirire? Ine ndikupepesa. Iwo awapeza iwo, ponseponse. Nambala firii, kodi mungabwere kuno, dona?

¹⁴⁶ Nambala foro. Ndani ali ndi khadi la pemphero nambala foro? Pitani kumeneko, dona. Nambala foro, kodi ndinawona zimenezo? Kodi ndi ameneyo...Ndani ali ndi nambala foro? Chabwino.

Nambala faivi, nambala sikisi, seveni, eyiti. Eyiti, nambala eyiti.

¹⁴⁷ Naini. Tsopano dikirani apa. Nambala eyiti, naini. Anthu ena atuluka, chotero mwina izo, akhoza kukhala amenewo. Nambala naini.

¹⁴⁸ Nambala teni, nambala leveni, nambala thwelofu, sartini, fortini, fifitini.

¹⁴⁹ Psyii! Ndiri ndi foro kapena faivi akusowa. Chotero tifika kwa izo. Mwinamwake anatuluka panja. Ngati aliyense abwera muno, M'bale Taylor, inu muyang'ane ndi kuwona ngati iwo ali ndi makadi apemphero kumeneko. Muwalowetse iwo mu mzere, ngati mungathe. Ngati mwina iwo anatuluka panja kumbuyo uko kwinakwake.

¹⁵⁰ Tsopano ine ndipempha kulemekeza kwathunthu, ndipo mungokhala molemekeza basi chomwecho.

¹⁵¹ Ndi angati muno akudwala ndipo alibe khadi la pemphero? Kodi mungakweze mmwamba manja anu ndi kuti, "Ine ndikudwala ndipo ndine wosowa ndipo ndiribe khadi la pemphero." Chabwino. Tsopano inu muyang'ane mbali iyi ndipo mukhulupirire. Chabwino.

Tsopano, M'bale Teddy, pang'onopang'ono kwenikweni.

152 Tsopano, ngati anthu awa salowa muno, ife tikhoza kupitirira ndi mzere wa pemphero, penapakenso. Koma tidikirira, kuti tiwapatse iwo malo.

153 Tsopano, ino ndi nthawi yomwe chirichonse chimene ine ndanena chikuyenera kuti chitsimikiziridwe kuti ndi cholondola kapena cholakwika. Kodi Baibulo silimanena kuti, “Tsimikizirani zinthu zonse. Ndipo gwiritsitsani kwa icho chimene chiri chabwino”? Tsopano ngati... Yesu, pokhala Mpesa wa Mulungu, wokutidwa pa Mpandowachifumu wa Mulungu, anabala Moyo Wamuyaya kwa Mpingo, ndipo ife ndi nthambi za Mpesa umenewo. Mukuona?

154 Iye anabzala Israeli ku Palestina. Izo sizinagwire ntchito. Iwo anadzakhala ngati... Zipatso zake zinafota ngati bowa. Izo zinakula usiku wonse, ndipo zinapita, zinawonetsera kuti sizinali zolondola. Analibe “Wamuyaya.”

155 Koma zipatso zomwe ziri mwa Khristu Yesu zidzakhhalapo kwanthawizonse. Izo zikuyenera kutero. Ndipo ngati Mzimu Wake, umene unali pa Iye, ukadali wamoyo lero, Iwo si chipembedzo chabowa. Iwo ndi Mulungu wamoyo amene amabala Moyo womwewo umene Iye ankawuchita. Inu mukukhulupirira zimenezo?

156 Tsopano, izo sizimangodzikweza ndi kuti, “Oh, zinthu zimenezo zinali za tsiku lina. Oh, Izo ndi chinachake chonga *ichi*.” Ngati izo zitero, inu muzulidwe, mmawa uno.

157 Ndi zenizeni. Ndi Moyo weniweni. Ndi Khristu weniweni. Tsopano inu mukhale ndi chikhulupiriro ndipo mukhulupirire, ndipo inu musati mukayikire ngakhale pang’ono koma kuti Mulungu alipo kuti achiritse odwala.

158 Tsopano, inu amene mulibe khadi la pemphero, ngati inu mungapemphere ndi kungokhulupirira ndi mtima wanu wonse, ndiye—ndiye Mulungu achita, Mulungu akupatsani inu zinthu zimene inu mukuzipemphazo. Ndi angati akukhulupirira zimenezo tsopano?

159 Tsopano ine ndikufuna ndikufunensi inu chinthu chimodzi chinanso. Ngati Mulungu angachite zoterozo... Tsopano tiyeni tiwone ngati pali aliyense mu mzere uwu yemwe ine ndikumudziwa. Palibe aliyense pamenepo amene ndikumudziwa.

160 Inde, Mlongo Logston. Kodi inu si Mlongo Logston? Ndi inuyo? [Mlongo Logston akuti, “Ine sindiri mu mzere.”—Mkonzi]. Oh, inu simuli mu mzere. Ine—ine ndikupepesa.

161 Ine ndikuganiza anthu amenewo onse ndi alendo kwa ine tsopano. Kodi uko—uko nkulondola? Sindikudziwa kanthu za inu. Kwezani manja anu mmwamba ngati izo ziri zoono. Pamenepo, izo zachitika motani? Basi izo zachitika motani, pongobwera pansu ndi kudzapereka mzere wonse wa makadi

apemphero, aliyense amene akuwafuna iwo pano, ngakhale kwa amene mwina anachita... ndi—akusowa? Kodi izo zinachitika motani? Mzere wathunthu pamenepo, palibe mmodzi muno tsopano mu kachisi. Ine sindikhulupirira kuti zimenezo zinachitikapo.

¹⁶² Tsopano inu amene mulibe khadi la pemphero. Analipo mkazi amene anakanikizira mchigulu, nthawi ina, ndipo anakhudza mphonje ya chovala Chake, pakuti iye anati, “Ine ndikukhulupirira. Sindikusamala zomwe wansembe akunena, kapena wina aliyense. Ine ndikumukhulupirira Iye. Ngati ine ndingakhudze chovala Chake, ine ndichiritsidwa.” Inu mukuidziwa nkhaniyo? Ndipo iye anakhudza chovala Chake. Ndipo Iye anatembenukira kwa iye ndipo anamuuzza iye kuti vuto la magazi lake lasiya. Chikhulupiriro chake chinamuchiritsa iye. Inu mukudziwa kuti zimenezo ndi Choonadi?

¹⁶³ Chabwino, Iye ndi Wansembe Wamkulu yemweyo mmawa uno. Iye ali pa Mpandowachifumu wa Mulungu. Mawu Ake, ndizo nthambi Zake. Mawu a Mulungu analumikizidwa pa Mpandowachifumu wa Mulungu maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Iwo anabweretsa Moyo, Khristu Yesu. Kudzera mu Moyo umenewo, anabweretsa nthambi, izo zikubweretsa Moyo womwewo umene Iwo uli kuchokera pa Mpandowachifumu. Nkulondola uko? Kenako Iye akukhala, chikhaliidwe cha mizu Yake lero, ali pa dzanja lamanja la Ufumu Kumwamba, kuti abweretse Moyo womwewo kudzera mu Mpingo Wake. Iye ndi Mkulu wa Ansembe amene angakhudzidwe ndi kumverera kwa zofooka zathu. Izo nzoona, sichoncho izo? Tsopano inu mukhulupirire izo ndi mtima wanu wonse.

¹⁶⁴ Ngati Iye achita ichi, ndi angati a inu odwala kunja uko mungavomereze izo? Nonse a inu? Tsopano, Teddy...

¹⁶⁵ Tsopano apa payima mkazi, yemwe anangokweza dzanja lake kuti ine sindimamudziwa iye. Ndipo Mulungu akudziwa zimenezo, monga momwe ine ndikudziwira, ine sindinayambe ndamuwonapo iye.

¹⁶⁶ Iye akhoza kukhala wochokera mu mzinda uno. Ine sindikudziwa. Sindikudziwanso gawo limodzi mwa magawo atatu a anthu. Anthu atsopano abwera. Ndinkakonda kupita kumusi kwa tawuni, ine—ine ndinkamudziwa aliyense. Tsopano ine sindikudziwa aliyense, nkomwe, chifukwa onse angobwera kumene.

¹⁶⁷ Ine sindikumudziwa mkaziyu. Iye sakundidziwa ine. Koma ngati Moyo womwewo umene unali mu Mpesa umenewo, umene unalonjeza kuti nthambi imeneyo idzabweretsa mzere womwewo umene a... Moyo womwewo umene Mpesa unabweretsa. “Iye amene akhulupirira mwa Ine, ntchito zimene

Ine ndikuzichita iyenso adzazichita.” Kodi limenelo ndi Lemba? Yohane Woyera 14:8. Chabwino.

¹⁶⁸ Tsopano, ngati ntchito imene Iye ankachita, anayankhula kwa mkazi pa chitsime ndipo anamuuzza iye chinachake chimene chinali chinthu chobisika mmoyo wake; ngati Mzimu Woyera womwewo, mmawa uno, ungagwire ntchito kudzera mu mpingo muno, ndi kuyankhula kudzera mwa ine, ndi kumuuzza mkazi uyu chinachake chimene iye wadzera pano, kapena chinachake chimene chakhala chiri mmoyo wake, kapena chinachake chimzake chimene iye akudziwa kuti ine sindikudziwa kanthu za chimo. Chifukwa, ngati ine sindikumudziwa iye, chabwino, ine—ine sindikudziwa chirichonse cha iye. Iye wangoyima apa.

¹⁶⁹ Koma ngati Mzimu Woyera umenewo upereka izo, mosalephera. Apa pali Mawu a Mulungu, analonjeza izo. Pano ife tonse tiri, tikunena, awiri tonse, “Ife sitinkadziwana wina ndi mzake, sitinawonanepo wina ndi mzake.” Ngati Mzimu Woyera uti uwulule izo, ndiye, Moyo womwewo umene unali mu nthambi imeneyo ukadali wamoyo, kapena mu Mpesa, kani, ukugunda kudzera mu nthambiyo. Mulole Ambuye Mulungu apereke izo.

¹⁷⁰ Tsopano, mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikutengera mzimu uliwonse muno pansa pa ulamuliro wanga, pa chifukwa cha Ufumu wa Mulungu. Tsopano, tsopano mungokhala molemekeza kwenikweni, aliyense.

¹⁷¹ Ife takomana kwa nthawi yathu yoyamba, mwamuna ndi mkazi, ndi chinachake monga izo zinali mu Lemba. Mulungu akuloleza izi, mwina, kuti anthu, pa Tsiku Lachiweruzo, azadziwe, asadzakhale ndi chowiringula. Ngati wina angachoke mmawa uno, popanda kubzalidwa mwa Khristu, popanda kudziwa ubwino Wake ndi chifundo Chake; popanda izo pamenepo, angadzakhale ndi mwayi wochepa kwambiri, ine ndingaganizire, pa Tsiku Lachiweruzo. Pamene Mawu alalikidwa, ndipo kenako ngati Mzimu Wake . . .

¹⁷² Mwaona, pali chinthu chimodzi, kulalikira chinachake. Ngati Iye ali Mulungu wa mbiriyakale, ndiye izo basi ndi zomwe Iye anachita mu mbiriyakale. Koma ngati Iye alidi Mpesa, ndipo ife ndi nthambi, ndiye nthambiyo ndi mochulukira basi gawonso. Moyo umene uli mu Mpesa ukugunda kudutsa mu nthambi, mwaona, chotero iyo ikuyenera kubala chinthu chomwecho. Iye analonjeza izo. “Iye amene akhulupirira mwa Ine, ntchito zimene Ine ndikuchita iyenso adzazichita.”

¹⁷³ Tsopano, ngati inu mukudwala, ndipo, izo—izo ine sindikudziwa. Koma ngati inu mukudwala, ine sindingakuchiritsemi inu, chifukwa Iye anachita kale izo.

¹⁷⁴ Koma zikhoza kukhala kuti Kukhalapo Kwake pano kungakupangitseni inu kumvetsa mwangwiro kuti Iye ali pano. Ndiye izo zingakweze chikhulupiriro chanu kuti muvomereze

izo. Mukuona? Umo ndi momwe chingachitire kwa omvetsera. Chimene chikanamuchitira mkazi uyu, chikanachita kwa aliyense wa inu. Tsopano mungokhulupirira zimenezo.

¹⁷⁵ Chifukwa, “Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu. Ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Ife tinali. Kale kwambiri, zaka thuu sauzande zapitazo, chipulumutso ndi machiritso zinabwera pamenepo.

¹⁷⁶ Tsopano inu mukuti, “Inu mukuyankhuliranj, M’bale Branham?” Ine ndikuwona zomwe Mzimu Woyera uti unene. Ine sindikumudziwa iye.

¹⁷⁷ Ndipo malo ovuta kwambiri omwe ine ndinayamba ndakhalapo nawo kuti ndikhale ndi msonkhano, ndi pomwe pano. Chifukwa, ndi zomwe Khristu ananena, “Mneneri m’dziko la kwawo, pakati pa anthu ake.” Mukuona zimenezo? “Iye anapita kwa Ake omwe, ndipo zinthu zambiri Iye sakanakhoza kuchita.” Iye anachokako. Tsopano, si chifukwa gulu laling’ono ili pano. Izo sindizo ayi. Mpingo wanga, iwo amandikonda ine ndipo amandikhulupirira ine. Koma ndi chinthu chakunjachi. Ndipo Mawu a Mulungu ananena. Iwo amanena choncho.

¹⁷⁸ Koma ine—ine ndayima kwa mphindi chabe, kuti ndiwone ngati Mzimu wa Mulungu ungandidzodze ine kuti ndifufuze. Tsopano, iye ndi mzimu ndipo iye ndi thupi. Tsiku lina mzimu udzachoka, ndipo zikadzatero thupilo lidzavunda. Mzimu umapita kwa Mulungu Amene amawupereka iwo. Apa pali mzimu, nawonso, wayima pano, koma iwo ukuyimiridwa mu thupi la mnofu. Tsopano ngati mizimu iyi ilumikizidwa mu Mpesa umenewo, iyo idzabala a . . .

¹⁷⁹ Ichu chinali chiyani? Pamene mzimu unabwera pamaso pa Yesu, umene panali chinachake cholakwika ndi iwo, Mzimu umenewo umene unali mwa Iye unawulula izo. Mukuona? Ndipo mkaziyo, pamene Iwo unawulula izo, iye anavomereza izo, ndipo anati, “Inu mukuyenera kukhala Mesiya. Ife tikudziwa kuti pamene Iye adzabwera, Iye adzatiuza ife zinthu izi.”

¹⁸⁰ Petro, pamene iye anabwera, oh, iye anakhala ngati anadabwa chimene Andreyka ankachikamba. Iye anati, “Iye ndi Mesiya.” Ndipo pamene iye anafika kwa Iye, Iye anati, “Dzina lako ndi Simoni. Ndiwe mwana wa Yonasi.” Zimenezo zinali zokwanira kwa iye. Mukuona? Iye ankadziwa kuti Iye sankadziwa yemwe iye anali.

¹⁸¹ Koma Iye akudziwa yemwe inu muli. Ine sindikudziwa yemwe inu muli, koma Iye akudziwa. Ine sindikudziwa kanthu za inu, koma Iye akudziwa.

Tsopano, ndi Uwu apa. Tsopano Mzimu wa Mulungu uli pano pa guwa.

¹⁸² Tsopano, ndiye, Inu mumadziwa kuti chinachake chachitika. Inu mwabwera pano chifukwa cha vuto lamanjenje. Uko

nkulondola. Inu muli ndi nyamakazi, nanunso. Izo nzoona. [Mlongo akuti, “Ndi choncho.”—Mkonzi]. Inu mukukhulupirira? Ine sindinamuwonepo mkaziyu mmoyo wanga.

¹⁸³ Tsopano, kodi zimenezo si zokoma, zenizeni zimenezo. . . Ine ndikudziwa inu mukuyenera kumvera Iwo. Ine ndikuyang’ana pa Iwo. Mukuona? Monga matsenga okoma.

¹⁸⁴ Ayi, ndikuwona mwamuna akubwera apa. Ndi mchimwene wanu. Inu mwakhala mukumupempherera iye mochuluka. Ine ndikumuwona wamng’ono, mwamuna wamng’ono. Iye akuyenera kukhala mtumiki. Ndi mwana wanu. Ali ndi vuto lauzimu. Inu mwachokera kutali, kuti mufike kuno. Inu mwachokera Kummwera, kubwera njira iyi. Ndinu wochokera ku Tennessee. Ndinu Akazi a Tabor. Bwererani. Mwapeza chopempha chanu. Mulungu wapereka icho kwa inu. Ngati. . .

¹⁸⁵ Tsopano, ine sindinamugwire konse mkaziyo. Mzimu Woyera wachita zimenezo. Tsopano, ndi zomwezo. Kodi ndi momwemo mmene zinachitikira mu Baibulo? Mkaziyo anati, “Inu mukuyenera kukhala Mesiya.” Tsopano, zimenezo sizikutanthauza kuti *ine* ndi Mesiya. Izo zikutanthauza kuti Mzimu wa Mesiya uli pano. Ndife amuna ndi akazi chabe. Ndi Mzimu wa Mesiya.

¹⁸⁶ Tsopano, inu mulandire Iwo, muzulidwe, kuchoka ku kusakhulupirira kwakale uko, ndipo mubzalidwe kumene ndi Iye, mwaona, tsopano. Dzukani nokha ndikuti, “Ambuye Yesu, Inu pokhala Mwana wa Mulungu, Wansembe Wamkulu. M’bale Branham anangoti Inu mwakhala mu Ufumu Kumwamba. Inu munakonzedweratu maziko a dziko lapansi asanak hazikitsidwe, Inu munaphedwa, kuti mudzabweretse zotsatira izi; kuti, ine, wokhulupirira watheka, ndikuyesetsa kuti ndikhulupirire, ndidzakhoze kupangidwa wathunthu kuti ndikhulupirire. Ndiroleni ine ndikhudze chovala Chanu. Mumulole iye kuti ayankhule ndi ine.” Inu amene. . .

¹⁸⁷ Inu mwa omvetsera, munene chinthu chomwecho. “Pakuti ngati Inu muli yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, Inu—Inu—Inu mundilole ine kuti ndikukhudzeni Inu ndi chikhulupiriro changa, kusiya pambali malingaliro onse a kusakhulupirira. Ndiroleni ine ndikukhudzeni Inu.”

¹⁸⁸ Ine ndikukhulupirira inu munakweza dzanja lanu, inunso, kuti ife ndi alendo kwa wina ndi mzake. [Mlongo akuti, “Ine ndinatero.”—Mkonzi]. Chabwino. Tsopano, ngati Ambuye Yesu angawulule kwa ine chinachake chimene chiri—chiri vuto ndi inu, kapena chinachake mwanjira ina, inu mungakhulupirire izo, kuti mzere wa Moyo uwu, kuti Mpingo wabzalidwa kwenikweni mwa Mulungu. Yesu anati, “Pa tsiku limenelo, inu mudzadziwa kuti Ine ndiri mwa Atate, Atate ali mwa Ine; ndipo Ine mwa inu, ndi inu mwa Ine.” Mukuona? Ndi Moyo umenewo wa Mulungu ukuyenderera mmusi kudutsa mu Dzina la Yesu

Khristu, mpaka mu Mpingo momwe, mwaona, zimatipanga ife mmodzi. Ndife nthambi. Ndife omuyimira Ake.

¹⁸⁹ Ngati inu mukukhulupirira zimenezo, vuto la phazi limenelo likusiyani inu. Kodi inu mungakhulupirire izo? [Mlongo akuti, “Ndikukhulupirira. Ndikukhulupirira.”—Mkonzi]. Chabwino. Inu mukhoza kukhala nazo. Ndipo mwamuna wanu kumeneko akhoza kuchiritsidwa, nayenso. Inu mukukhulupirira iye angatero, za chophukacho? [“Inde.”] Inu, bwana, mukukhulupirira kuti inu muchiritsidwa? [M’baleyo akuti, “Ameni.”] Uh-huh. Inu mukutero? Muli ndi mwana wamkazi, nanunso. Iye ali ndi mzimu wa vuto lina lauzimu. Inu mumachokera Kumpoto, kubwera njira iyi. Inu mwadzera mu msewu waukulu. Ndinu wochokera ku Austin. Dzina lanu ndi Akazi a White. Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. [“Oh!”] Bwererani ndipo mukhulupirire tsopano, ndipo muchiritsidwe, ndipo mukakhale bwino. Mulungu akupatseni inu chokhumba cha mtima wanu.

“Ngati mungakhulupirire, zinthu zonse ndi zotheka.”

¹⁹⁰ Moyo wa Moyo wa Khristu, mu nthambi. Nthambiyo si Branham Tabernacle. Nthambiyo si William Branham. Nthambiyo ndi aliyense amene azulidwa kuchoka mu kusakhulupirira kwanu, ndi kudzabzalidwa mwa Iye.

¹⁹¹ Ine ndikukhulupirira inu munakweza dzanja lanu kuti, ifenso, ndi alendo. Ine sindikukudziwani inu. Mulungu amakudziwani inu. Simunabwere kuno chifukwa cha inunwini. Ndi chifukwa cha mwana. Ine ndikuwona Kuwala kukulendewera pa mwanayo. Ngati Mulungu angawulule kwa ine chimene chiri cholakwika ndi mwana wanuyo, kodi inu mungandikhulupirire ine kuti ndine mneneri Wake, ndi kukhulupirira kuti Ine ndikukuuzani inu choonadi? Inu mutero. Mwanayo ali ndi vuto la mtima. Ndi chinachake chonga valavu, adokotala anatero. Izo zinawunikidwa. Iye akufuna kumutumiza iye ku chipatala nthawi yomweyo. Uko nkulondola. Ndinu wochokera kuno ku Jeffersonville, cha kuno pa msewu, Fulton Street. Koma ndiko kulondola. Ndipo dzina lanu ndi Akazi a Burkhart, Irene Burkhart. Bwererani, ndipo mukhulupirire mmalo mwa mwanayo, iye akhala bwino.

¹⁹² “Ngati mungakhulupirire, zinthu zonse ndi zotheka.” Ngati mungakhulupirire!

¹⁹³ Mkazi yu wakhala apa ndi vuto lamanjenje limenelo. Inde. Iwalani zimenezo. Inu mukupita kwanu, kakhaleni bwino tsopano.

“Ngati inu mungakhulupirire!”

¹⁹⁴ Munakweza dzanja lanu mmwamba monga *chonchi*, muli ndi vuto la nsana. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani inu? Inu mukukhulupirira, mukuvomereza

zimenezo? Ndiye pitani kwanu ndipo mukakhale bwino. Yesu Khristu wakuchizani inu.

¹⁹⁵ Lanu ndi impsyo. Chotero, zipitirirani, mwalandira lanu, inunso, bwana. Mulungu akudalitseni.

Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Musakayikire.

¹⁹⁶ Mkazi wachikuda. Pali awiri a iwo. Kumbuyo komwe kumbuyo uko. Chotupa ku mmero, pa mmero. Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse. Inu mukukhulupirira zimenezo, dona? Chowoneka ngati chipewa chaching'ono, pamenepo. Inu mukukhulupirira? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Chabwino. Pitani kwanu; icho chikusiyani inu.

¹⁹⁷ Pali mkazi wamng'ono kumuposa uyu. Ine sindikukudziwani inu. Mulungu akukudziwani inu. Inu mukukhulupirira kuti Iye akhoza kukupangani inu kukhala bwino? [Mlongo akuti, "Inde."—Mkonzi]. Chabwino, bwererani ku New Albany, Abiti Pearl Allen, ndi muchiritsidwe. Yesu Khristu wakuchizani inu. Inu kazipitani, mukukhulupirira izo, inu mukhoza kukhala bwino.

¹⁹⁸ Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. Inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Tsopano, sichoncho... Oh, chirichonse chikuchitika basi, pa... Ngati iwe ungakhulupirire izo, mzanga!

¹⁹⁹ Muli bwanji, bwana? Inu mukumukhulupirira Yesu Khristu Mwana wa Mulungu? Inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri Wake? [M'baleyo akuti, "Ine ndikutero."—Mkonzi]. Inu mukukhulupirira kuti chimene ine ndingakuuzeni inu. Inu mungadziwe ngati icho chiri choona kapena ayi. Inu mukukhulupirira kuti zimene ine ndalalikira, mmawa uno, ndi Choonadi? ["Inde."] Inu mukukhulupirira. Muli pano chifukwa cha chinthu chabwino. Muli pano kuti mudzachtose chizolowezi, ndicho, kusuta. Ine ndikukuwonani inu mukuyang'ana pa icho, ndi kuchitsutsa chinthucho, ndi kuchichotsa icho kwa inu. Uko nkulondola. Musatero... ngati inu... Mvetserani. Inu mukufuna pemphero kwa mkazi wanu. Iye amakhala ngati ndi chizungulire. Bambo Carlock, bwererani ku Owensboro, Kentucky, kumene inu mukuchokera. Musakagwirensa yina. Yesu Khristu wakupangani inu wathunthu. Pitani, mu Dzina la Ambuye, ndipo muchiritsidwe.

Inu mukukhulupirira?

²⁰⁰ Tsopano taonani. Mwamuna uyu akubwera apa, mungoyika dzanja lanu pa langa, bambo, apa. Vuto lanu la nsana latha. Basi kazipitirirani mudutse pamenepo, mukumuthokoza Mulungu. Amen.

²⁰¹ Mukufuna kuti mupite mukadya chakudya chanu chamadzulo? Vuto la mmimba likusiyani inu ngati inu mukukhulupirira izo. Inu mukukhulupirira zimenezo?

Zipitirirani panjira yanu. Mungolemekeza Mulungu, ndi kuti, “Zikomo Inu, Ambuye.”

202 Ndi angati akukhulupirira ndi mtima wanu wonse?

203 Mulungu akudalitseni inu. Monga choncho, inunso, inu mukhoza kupita ndi kukamutamanda Ambuye. Nenani, “Zikomo Inu, Ambuye.”

204 Inu muli ndi vuto limene anthu ambiri kunjira kuno ali nalo. Ndi manjenje, zimapangitsa mtima wanu kumapitirira, ndi vuto la mtima. Ngati inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse!

205 Kunja uko, ndi angati ali ndi mtima wamanjenje ndi zinthu? Tsopano kwezani manja anu monga *choncho*. Yang’anani kunjira kuno. Inu mungathe kuzitchula izo motani? Mukuona?

206 Inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Inu mukutero, inunso? Chabwino. Pitani ndipo mukachiritsidwe mu Dzina la Yesu Khristu. Musakayikire pang’ono, koma mukhulupirire mu zomwe zananedwa kwa inu kuti ndi Choonadi. Mukhulupirire kuti mwachiritsidwa. Mudzapeza zimene mwapemphazo.

207 Nonsenu muchite chimodzimidzi. Ndi angati ena a inu kunjira kuno omwe muli nawo iwo? Chabwino, bwana. Ndi angati kunjira uko akusowa Mulungu? Kwezani mmwamba manja anu. Ndipo munene. . .

208 Penyani. Mvetsani ichi. Ine sindingathe kuchiritsa aliyense. Ndine munthu. Ngati Khristu akanayima pano, Iye sakanakhoza kuchiritsa aliyense wa inu. Iye wayika dongosolo, ndipo dongosolo limenelo ndi lakuti inu mukhulupirire kuti Iye anakuferani inu, inu mukhoza kuchiritsidwa ndi zimenezo. Ndiyo njira yokhayo. Ndi machiritso a chikhulupiriro. Chikhulupiriro! Mukhulupirire kuti Khristu wakulupirirani inu mtengo. Ndi angati akumvetsa zimenezo tsopano? Chabwino. Ndi angati akuvomereza zimenezo? Chabwino.

209 Pamene ife tikupemphera, ikani manja anu pa wina ndi mzake. Ikani manja anu pa wina ndi mzake, aliyense apemphere.

210 Tsopano inu mukhoza kupita pa mpando wanu, mlongo. Mulungu akudalitseni inu tsopano. Mukhale bwino...?... Inde. Uko nkulondola. Ndi vuto la manjenje, koma ilo—ilo likusiyani inu. Yendani kudutsa pamenepo tsopano, muwone ngati izo. . . Mwayamba kumverera mosinthika, sichoncho inu? Mukuona? Ndithudi. Inu munachiritsidwa, mutayima pomwe pano. Inu munazindikira momwe iye amachokera pa sitepeyo ndiye popanda izo? Mukuona? Ndipo tsopano inu muli bwino. Tsopano inu mukhoza kupita kwanu, mukakhale bwino. Ambuye akudalitseni inu.

211 Tsopano ndi manja anu pa wina ndi mzake. Mwaona, ife tiribe nthawi yochulukira, ndi pafupifupi masana. Ndipo iwo ali ndi utumiki wa ubatizo, apobe.

212 Ndithudi, ndithudi, anthu, Moyo wawukulu wa Mulungu, Mzimu Woyera wawukulu Umene unawonetsera mosalephera kuti Iye ali pano, ukuwonetsera kuti Moyo umenewo umene ukuchokera ku Mpandowachifumu wa Mulungu ukugundira mu nthambi, kuti uwonetsera Moyo. Kodi inu simukukhulupirira zimenezo? Ndiye, ayi, ine sindinachiritse aliyense wa anthu awa amene anabwera kuno. Chikhulupiro chawo chachita zimenezo chifukwa iwo anauzidwa chinachake chimene chiri choonadi. Ngati inu mukanakhala pano, Iwo ukanachita chinthu chomwecho.

213 Tsopano kwa inu kunja uko, Iye akuwululira kwa inu chimene inu mukusowa. Tsopano pamene ife tikupemphera, tonse pamodzi, pempherani, inu mukhulupirire mawu aliwonse kuti ndi owona, ndipo muwone chimene chichitike. Inu muchiritsidwa. Tsopano inu mumupempherere munthuyo. Musadzipempherere nokha. Mupempherereni munthu amene mwayikapo manja anu. Mulole munthu ameneyo akupempherereni inu. Kupemphererana wina ndi mzake. Baibulo limanena izi tsopano.

214 Baibulo lomwelo lomwe linati, “Ntchito zimene Ine ndikuzichita inunso mudzazichita,” linanena izi, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Ngati iwo adzayika manja awo pa odwala, iwo adzachira.” Tsopano, Mulungu amene anapanga lonjezo limodzi, ndipo amalisinga ilo, ngati inu munabzalidwa mmenemo, pa mitsinje ya Madzi, Iwo amabweretsa Kukhalapo Kwaumulungu kulikonse kwa Mulungu, lonjezo lirilonse, mu chilumikizo chanu momwe. Ndinu mtengo wobzalidwa mmphepete mwa mitsinje ya Madzi amodzi. Madzi amodzi amenewo ndi Khristu, Mzimu Wake Woyera. Pali machiritso. Pali chipulumutso. Pali chisangalalo. Pali kulezamtima, kufatsa, kudekha, chipiriro. Mitundu yonse ya mphatso ziri mu Dzina limodzi lofunika limenelo. “Chirichonse chimene muwapempha Atate mu Dzina Langa, icho Ine ndidzazichita.”

215 Tsopano inu mupemphere mu Dzina la Yesu, kwa munthu amene inu mwayikapo manja anu. Ine ndikupemphererani nonsenu, kwa inu nonse. Mulole Mzimu Woyera, umene ulipo tsopano, uchize munthu aliyense.

216 Ambuye, ife tikupempha kuti kukoma mtima Kwanu kupitirire ndi ife. Aliyense akupemphera mwanjira yake yomwe. Iwo awuwona Mzimu wa Mulungu wamoyo ukupangidwa weniweni monga momwe Iwo unaliri ku Galileya. Basi monga momwe Iwo unaliri pamene Petro anabwera kumeneko mmphepete mwa Galileya, ndipo Yesu anamuuzza iye yemwe iye anali. Ndipo zenizeni basi monga zinaliri pamene Nataniele anabwera, ndipo Iye anamuuzza iye kumene iye anali dzulo lake. Zenizeni basi monga zinali pa chipata cha Samariya, kapena

pa chitsime. Ndithudi anthu akanatha kunena kuti, “Uwu ndi Mzimu wa Mulungu wamoyo.”

²¹⁷ Ambuye, perekani chikhulupiriro ndi kukhalapo kwa malingaliro, ndi Kukhalapo kwa Mzimu Woyera, kuti aliyense, akupemphera, akhoze kumupempherera mzake, pemphero la chikhulupiriro. Ine ndikupempha tsopano, Ambuye, chifukwa cha iwo amene manja awo ali pa winawake, kuti Inu muwapatse iwo chikhulupiriro chosasintha, pakali pano kwa munthu ameneyo. Ndipo, ndithudi, izo zibwerera kwa iwo. Oh, mulole izo zikhale! Ambuye Mulungu, mulole izo zikhale. Ife tikhoza kuwabweretsa iwo, mmodzi ndi mmodzi, kudutsa pa nsanja, ndi chotsatira chomwecho; komabe izo zimatengera chikhulupiriro, chikhulupiriro mwa munthu payekha, kuti akhulupirire Mulungu. Ndipo kwalembedwa, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Ngati iwo adzayika manja awo pa odwala, iwo adzachira.”

²¹⁸ O Ambuye, musunge lonjezo Lanu mmawa uno, kwa wokhulupirira aliyense. Ndipo mulole Mzimu Woyera tsopano ungosuntha kulowa mmaturi a anthu odwala awa, ndi kuchotsa kudwala konse ndi matenda. Mulole pakhale kutsimikizira kwa izo koteroko mpaka mitima ya anthu amenewo idumphe ndi chisangalalo, kukhulupirira kuti Mulungu wawachiritsa iwo. Mulole iwo apite kuchokera pa kachisi uyu, akuyimba ndi kusangalala, ndi kukhulupirira kuti Mulungu wawapanga iwo amphumphu. Mulole iwo adzabwerenso pa tsiku lina, osangalala, okondwa, akuchitira umboni, monga mahandirede akhoza kuchitira umboni lero kuzungulira dziko, za Mphamvu Yanu yochiritsa. Pemphero ili ife tikulinena pa anthu awa, kupempha kuti zikhale chomwecho, mu Dzina la Yesu Khristu Mwana wa Mulungu. Mulole Kuwala kwa Mulungu kutulukirie ndi kuchiritsa onse. Amen.

Ndikhoza, nditero, ndikukhulupirira;
 Ndikhoza, nditero, ndikukhulupirira;
 Ndikhoza, nditero, ndikukhulupirira
 Kuti Yesu wandichiza tsopano.

Kodi mukuchita zimenezo? Kwezani dzanja lanu.

Ndikhoza, nditero, ndikukhulupirira;
 Ndikhoza, nditero, ndikukhulupirira;
 Ndikhoza, nditero, ndikukhulupirira
 Kuti Yesu wandichiza tsopano.

[Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]...khulupirirani zimenezo.

²¹⁹ Ine ndimakhoza kucheza nyumba za anthu, ndipo iwo amakhoza kuphika chakudya chamadzulo chabwino. Amachita kundiwiritsira ine kapu ya madzi otentha, ndi kundikhasika ine panso pafupi ndi msuzi pang’ono wa barele; iwo ali ndi mitundu yonse ya zinthu zabwino pa tebulo. Tsiku lina ine ndinati

kwa Ambuye, “Ine ndikukhulupirira. Ine ndikukhulupirira.” Oh, mai! Ndinayenda ndikutsikira kumusi mumsewu ndi chakudya changa choyamba chodzaza mkamwa chiri m’ mimba mwanga, ndikuyimba:

Ndikhoza, nditero, ndikukhulupirira;


Icho chinkayesa kubwera mmwamba; ndinkachibwezanso.

Ndikhoza, nditero, ndikukhulupirira;

Ndikhoza, nditero, ndikukhulupirira

Kuti Yesu wandichiza tsopano.

²²⁰ Inde. Izo zakhala zaka ziri twente-faivi zapitazo. Iye wakhala weniweni kwa ine kuyambira nthawi imeneyo. Ndine wothokoza kwambiri chifukwa cha izo. Mulole chikhale chinthu chomwecho kwa inu. Mulungu akudalitseni inu.

²²¹ Tsopano iwo akhala ndi utumiki wa ubatizo, mu maminiti pang’ono chabe, ine ndikukhulupirira; eya, ndi zimenezo, ngati alipo ena pano oti abatizidwe mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Ngati alipo anthu oterowo, kuchitira kuti tidziwe ngati tiwabalalitse omvetserawa kapena—kapena kuwagwira iwo pang’ono chabe, kodi inu mungakweze manja anu ngati winawake ati abatizidwe mu Dzina la Ambuye Yesu? Wani, thuu, firii, foro. Chabwino. Ngati akazi angapite mbali iyi *apa*, ndi amuna cha *apa*, kuti akakonzekere, ngati inu mungathe. Pamene ife tikuyimba kamodzinsu, I . . . 

59-0920 Kubzala Mpesa Ndi Komwe Mungawubzale Iwo
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org